

KODI MELKIZEDEKI UYU NDI NDANI?



Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu kwa pemphero.

Okonedwa Atate Akumwamba, ife tikayimva nyimbo iyi ya *Kungokhulupirira*, iyo imatipangitsa ife kudziwa kuti ndicho chonse chimene ife tiyenera kuchita kuti tilandire lililonse la malonjezo a Mulungu, kungowakhulupirira iwo. Pakuti izo zinalembedwa, “Zinthu zonse nzotheka kwa iwo amene akhulupirira.” Pamene ife tikulira, monga mwamuna yemwe anali naye mwana wakhunyu, “Ambuye, ine ndikukhulupirira! Thandizani Inu kusakhulupirira kwanga.”

² Ife tikukuthokozani Inu chifukwa cha mphamvu Yanu yayikulu, vumbulutso Lanu lalikulu la Inueni kwa ife mu masiku otsiriza awa. Izo zimapangitsa mtima wathu wokondwa kwambiri ndi wosangalala, kudziwa kuti ife tabwera mu kukhudzana naye Mulungu wamoyo; Amene amatimikiziranso izo mu thupi kumene, maumboni ogwirika, monga Iye anachitira mu masiku amene apitawo, ndipo monga Iye walonjezera kwa tsiku ili. Ife tiri oyamikira kwambiri kwa Inu, Mulungu wathu. Tsiku la mdima ili limene palibe amene akuwoneka kuti akudziwa njira yoti apite, ife tiri okondwa kwambiri kuti ife tinapeza malo a chitetezero, kothawirako.

³ Tsopano tidalitseni ife usiku uno, Ambuye, pamene ife tikulankhula za Mawu Anu. Ndipo malonjezo amene aperekedwa kwa ife, titawasunga iwo mu mitima yathu, kuwasamalira iwo ndi ulemu, ndi kuwamvera iwo ndi ulemu weniweni waumulungu. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

⁴ [Winawake akulankhula kwa M'bale Branham—Mkonzi.] Chopereka chachikondi? Iwo sakanatero—iwo sakanachita izo. Ndani anachita izo? Ndinu olakwa? Ine ndimawapanikiza a manenjala. Iwo ananena kuti ananditengera ine chopereka chachikondi. Iwo akanati asachite izo. Ine ndikuyamikira izo, Mulungu akudziwa izo, koma ine—ine sindimabwerera konse izo. Zikomo inu. Ambuye atakudalitsani inu. Inu ndidzachita chirichonse chimene ine ndingakhoze. Ine ndidzaziika izo mu umishoni wa kunjja, kotero ine ndidzadziwa kuti izo zidzapita ku Ufumu wa Mulungu. Ndipo ngati Ambuye alola, ine ndidzazitengera izo, inemwini, kumaiko, kukabweretsa Uthenga womwewu umene inu mwakhala mutakhala, mukuwumvetsera sabata ino, ndiye ine ndikudziwa kuti izo zidzachitika momwe

inu mwakhala mukukhulupirira Iwo. Ambuye andithandize ine kuchita izo.

⁵ Ine ndiri wokondwa kwambiri chifukwa cha kubwera kwakukulu sabata ino, ndi chifukwa cha inu anthu nonse amene mukumvetseranso usiku uno ndi—mawaya a telefoni. Ndipo ife tiri othokoza kwa wina ndi aliyense wa inu.

⁶ Billy ananena kwa ine mmawa uno, iye anati, “Adadi, ngati inu mukanabwera ndi ine mmawa uno, molawirira, kutangocha kumene, ndikuyima kunjira kuno pozungulira mmalo awa ndi kuwawona amayi akudyetsa ana awo mgalimoto, anthu osauka awo atakhala mu mvula ija, kuyembekezera kuti zitseko zitsegulidwe!” Inu mukuona chimene wachinyengo ine ndingakhale ngati ine nditakuuzani inu chirichonse osakhala Choonadi? Ine ndingakhale kwenikweni munthu woyipa. Nthawizina ndimayenera kuwapweteka, koma sindicho chifukwa chakuti ine ndimafuna kutero, ndicho chifukwa... Sindine amene ndimawapweteka. Ndi Choonadi chimene chimawapweteka. Ndipo ine—ine... Koma ine ndikukhulupirira kuti ndicho chifukwa inu mumabwera, chifukwa ine ndiri wowona mtima kwenikweni ndi inu, ndipo ndimachita zonse zimene ine ndingathe kuti ndikuthandizeni inu. Ambuye athandize wina aliyense wa inu.

⁷ Ndipo tsopano ine ndikufuna ndithokoze anthu chifukwa cha chigwirizano chawo chabwino, anthu a mzindawu kuno, nawonso, amene anatipatsa ife, kutilola ife kuti tikhale nako kubwereka kwa nyumba ya sukulu iyi, nyumba yochitira msonkhano ino ndi nyumba ya masewero. Ndipo ine ndikufuna kuthokoza olemekeseka ngati inu muli pano. Ndiponso ine ndikufuna kuthokoza Houston Colvin, yemwe ali wosamalira pano, chifukwa cha chiyanjano chake chabwino mu kutithandiza ife kuti tipeze awa ndi pokhala nafe ife usiku uliwonse.

⁸ Ife tikuthokoza a polisi ya Jeffersonville chifukwa chobwera kuno ndi kuyang’anira, ndi mtengo wotsika kwenikweni. Ine ndikuganiza pafupi madola awiri pa ora, momwe apolisi anayikidwa pano pa ntchito yapadera, kuti azisanjitsa magalimoto, kuwona kuti panalibe...popanda chochitika, ndipo chirichonse chinali bwino. Ndife othokoza kwa anthu chifukwa cha izo. Ndipo kwa—a, nawonso, a injiniya kuno pa—gulu, ine ndamuzindikira iye. Ndipo onse amene akhudzidwa nazo izi, ife ndife othokoza kwenikweni kwa inu.

⁹ Ine ndikuthokoza wina aliyense wa inu chifukwa cha mphatso. Billy wandibweretsera kumene ine, madzulo ano, m—mphatso, zingapo za izo, ndi mabokosi, suwiti, ndi zina zotero. Ndipo ina ya iyo inali m—Madalitso, ndi chithunzi cha Khristu atajambula mu icho—icho, Ulaliki wa pa Phiri. Ndipo icho ndithudi chinali chokongola. Ine ndithudi ndikukuthokozani

inu. Ndi zinthu zambiri zotero, ine sindikudziwa momwe ine ndingakuthokozereni inu chifukwa cha izo. Ndiyeno, ndiponso, chifukwa cha kwanu—kuthandiza kwanu, kuthandizira mu chuma msonkhano, ife ndithudi tikuyamikira izo, ndi mtima wathu wonse. Ambuye adalitse aliyense wa inu, molemerera.

¹⁰ Billy anati, panali anthu ambiri, inu mwakhala mukupempha zolankhulana zapadera pa nthawi iyi. Ndipo ambiri anapempha ndipo anali nawo ana aang'ono oti adalitsidwe. O, momwe ine ndikufunira kuchita izo!

Koma, inu mukuona, pamene ine ndinabwera nthawi iyi, ndi zofulumira kwambiri. Ine ndiyenera kukhala molondola, nthawi zonse, mu kuwerenga, Mawu awa ndi pemphero, pa chifukwa chobweretsa Mauthenga awa. Onani, iwo sali. . . Iwo ali—iwo ali achirendo kwa ife, chifukwa ndiko kupeza chifuniro cha Mulungu ndiyeno kulankhula zinthu. Ndi zonse zomwe ziyenera kukomana palimodzi, ndi kumupempha Mulungu chabe chimene ndiyenera kutsegula.

¹¹ Tsopano, Ambuye akalola, ife tidzabwereranso posachedwapa, mwamsanga pamene ife tikhoza kupeza tsiku. Ine ndinapanga ku—kusuntha, kapena—kapena ananena chinachake za Isitara. Ine kulibwino ndifufuze izo, chifukwa ine ndikuganiza ndiyenera kukakhala mu California motsatira pafupi nthawi imeneyo. Kotero izo mwina zikhoza kukhala zolakwika. Komabe, pamene ife tidzabwereranso ku kachisi, ife tidzakutumizirani inu khadi, ndi mpingo, ndi—ndi kukupatsani inu—tsiku ndi nthawi. Ndiye ine ndidza, mwina panthawi imeneyo, kachiwiri. . .

¹² Ine sindinayike nthawi iliyonse yopempherera odwala. Ife sitinakhale nawo msonkhano umodzi umene ife tinabweretsa anthu ndi kuwapempherera iwo. Ife takhala tikuwatumiza iwo kunjira. Ndipo abale athu pano akhala akulalikira, M'bale Lee Vayle ndi M'bale. . . Abale ena awa akhala akulalikira, ndi kupempherera odwala, ndi kuchita ubatizo wa madzi, kubatiza, kani, ndi kundirola ine kukhala ndekha ndi Mawu. Ife tikuthokoza amuna awa. Iwo anachita ntchito yayikulu.

¹³ Pali abwenzi ambiri pano amene ine ndikufuna kukomana nawo. Ine ndikuyang'ana pansi ndikuona John ndi Earl. Ndipo apa pali Dotolo Lee Vayle, mmodzi wa mamananjala a msonkhano. M'bale Roy Borders. Amuna awo, ine ndiribe ngakhale. . . Ine sindinagwedeze ngakhale dzanja lawo. Ine sindinakhale nawo mwayi kutero. Ine ndikuganiza za amzanga ochokera ku Kentucky, ndi ozungulira kuno, ndi amzanga otumikira, momwe ine ndikufunira kuwagwira manja awo! M'bale Blair, ine ndinamuzindikira iye kuno tsiku lina. Ndi ochuluka a anthu awo omwe ine—ine ndimawakonda, ndipo iwo akhalapo ku misonkhano yambiri, ndipo ine sindinali ngakhale mochuluka monga kugwedeza dzanja lawo. Ine—

ine ndikuyesera. . . Izo siziri chifukwa chakuti ine sindikufuna kuchita izo; ndizo chifukwa chakuti ine ndiribe nthawi yochitira izo, ndipo ine ndikungofulumira.

¹⁴ Kudalitsa ana, zedi. Mwana wamwamuna wanga yemwe, mdzukululu wanga wamwamuna wamng'ono amayenera kuti adalitsidwe pa msonkhano uwu. Ine sindinakhale nayo nthawi kuti ndichite izo; David wamng'ono. Ndine agogo, kawiri tsopano. Kotero, Bambo May, ngati iwo ali pano usikuuno, amene anandipatsa ine ndodo ija, zikuwoneka ngati ine ndidzayenera kuyigwiritsa ntchito iyo posachedwapa.

¹⁵ Kotero, ndipo ine ndinamuza Billy, ine ndinati, “Baibulo linanena kuti chulukanani ndi kudzadzitsa dziko lapansi, koma ntchito yonseyo siyinapatsidwe kwa iwe.” Ndipo zidzukululu zachimuna izi zikuwoneka mofulumira.

Ndipo kotero, kumbukirani, mpongozi wamkazi wanga anali chumba, kuyamba ndi kuyamba. Iye sakanakhoza kukhala nawo ana. Ndipo tsiku lina, akuchoka mu msonkhano, Ambuye analankhula nane ndipo ndinati, “Loyce, iwe udzabala mwana wa mwamuna. Ambuye akudalitsa iwe. Vuto lako lachikazi latha.” Paul wamng'ono anabadwa, miyezi isanu ndi inayi yotsatira.

¹⁶ Miyezi iwiri mwana uyu asanadze powonekera, ine ndinali nditakhala, ndikudya kadzutsa mmawa wina, pa thebulo, ndipo Loyce ndi Billy anali atakhala pozungulira thebulo kwa ine. Ndipo ine ndinamuwona Loyce akudyetsa mwana wamng'ono ndi pinki. . . kapena bulangeti la buluu atamukulungamo iye. Ndipo Billy anali atakhala pangodya, akudyetsa Paul wamng'ono. Ine ndinati, “Billy, ine ndawona kumene masomphenya. Loyce anali kudyetsa mwana atamukulunga mu bulangeti la buluu.”

Iye anati, “Ndi umenewo ulendo wanga wokasaka. Ndiyo miyezi isanu ndi inayi chabe kuchokera tsopano.”

Miyezi khumi ndi umodzi kenako, Davide wamng'ono anabadwa. Ndipo ine sindinakhalebe wokhoza kumudalitsitsa iye kwa Ambuye, ndipo sindidzatero mpaka ife titabwereranso. Kotero inu mukuona chimene icho chiri.

¹⁷ Momwe ine ndimawakondera anthu ndi chiyanjano chawo! Koma abale athu akhala akupempherera odwala, ndipo ine ndikudziwa kuti ndi chopambana. Usiku uliwonse ife tapempherera odwala, wina kusanjika manja ake pa wina, tonse a ife palimodzi, chimene njira iyo chimagwira mawonekedwe onse. Koma mwina, ngati Mulungu alola. . . Ine ndidzasonyeza izo pa khadi, ngati ife titumiza ilo. Pobwereranso, ine ndikufuna kudzapereka pafupi masiku awiri kapena atatu, kachiwiri, basi kupempherera odwala ndi kuchita zimene ife tingakhoze mmakhalidwe awo. Tsopano, ndipo ine ndikuthokoza anthu chifukwa cha thandizo lawo, kachiwiri.

18 Tsopano ine ndikungofuna kuchitira ndemanga, mphindi chabe, pa—pa Uthenga wa mmawa. Palibe kukayikira, ine sindinapyolemo mwathunthu ndi iwo, koma ine ndikuganiza inu mukumvetsa. Ndipo ine ndikutsimikiza kuti inu simunatero . . . Inu simudzadziwa konse chimene icho chinali choti ine ndichite.

19 Tsopano, izo zikuwoneka zophweka kwambiri kwa inu. Koma, inu, inu mukuona chimene inu mukuchita? Inu mukutenga malo a Mulungu, kuti munene Chinachake. Ndipo ine ndisanachite icho, ilo linayenera kubwera yankho kuchokera kwa Mulungu. Ndipo Iye anachita kubwera pansu, ndipo Iye mowonekera anadziwonetsa Iyemwini, napereka Vumbulutso. Chotero, onani, izi ndi za kwa Mpingo. Ndipo kumbukirani, ine ndinati, “Izi, ichi chimene ine ndinanena, chinali kwa Mpingo wokha.”

20 Ndipo kotero kuti inu mukhale nacho chidaliro ndi kudziwa, ameneyo anali Mulungu yemweyo amene ananena kwa ine pamwamba paja pamene panalibe agologolo. “Lankhula, ndipo unene pamene iwo ati akhale.” Ndipo nthawi zitanu zolunjika izo zinachitika. Tsopano, ngati Iye angakhoze mwa mawu omwewo kulenga chinachake chimene palibe apo, mochuluka bwanji momwe Ichi chiti chidzagwirire zolimba pa Tsiku la Chiweruzo! Mwaona? Anthu anali pamene kuti awone zinthu izi, ndi kudziwa. Monga Paulo ananena, mmasiku apitawo. Pali munthu ali naye iye, amene—amene anamverera kugwedeza kwa dziko lapansi; ndipo sanamve liwulo, koma iwo—iwo anawona—Lawi la Moto.

21 Izo zinandichitira ine zabwino, ngakhale, zitatha izo; kuwona amuna ndi akazi, amene ine ndikuwadziwa kuti ali Akhristu enieni, akukumbatirana wina ndi mzake namalira.

22 Ndipo mverani, amzanga, Mulungu amatsimikizira Mawu Ake ndi zizindikiro ndi zitsimikizo, kutsimikizira kuti Ndi zolondola, Mawu olankhulidwa. Tsopano kumbukirani, Kuwala kuja kumene kunali mu Mtambo uja, kumene kunapereka Vumbulutso. Ine ndinali . . .

Msungwana wanga wamng’ono anali kundiwuza ine, Sarah apa, kuti pamene iwo . . . Sukulu ija uko mu Arizona anali kuyang’ana pamwamba apo mumlengalenga mopanda mtambo, ndi kuwona Mtambo wachinsinsi uwu mu phiri lija, ukutsikandi-kumakwera, ndi Moto wa ambara ukuyaka mkati mwa Iwo. Aphunzitsi anabalalitsa makalasi ndi sukulu, ndi kuwabweretsa iwo patsogolo, ndi kunena, “Kodi inu munayamba mwawonapo chirichonse chonga icho? Taonani momwe icho chiriri apo.”

Kumbukirani, ndiko Kuwala kwa ambala komwe kuja kumene kuli pa thanthwe. Kotero ali Mulungu yemweyo, Vumbulutso lomwelo, anati, “Awuze iwo kuti achite *izi*.” Ndizo zimene ine ndinakuuzani inu mmawa uno, kotero ndi Izo apo.

²³ Ngati zitapezeka kuti mzanga wabwino, M'bale Roy Roberson, akumvetsera ku Tucson. Roy, iwe ukukumbukira, tsiku lina, masomphenya amene iwe unawawona pamene ife tinali kunja titayima pa phiri? Iwe unabwera kwa ine, ndipo Mtambo uja unali pa mthobo? Ukubwera choyenda pansi, iwe ukudziwa chimene Iye anakuwuzwa iwe; ndipo ine ndinakuwuzwa iwe pa nyumba ija, tsiku lina? Ndizo izo, Roy. Usadandaulenso, mwana. Izo zatha.

²⁴ Iwe sukudziwa basi chomwe izo zikutanthawuza! Ndicho chisomo. Iye amakukonda iwe. Ndipo iwe umukonde Iye, modzichepetsa umutumikire Iye ndi kumupembedza Iye masiku ako onse. Khala wokondwa, pitirira ndi kukhala moyo monga iwe uli. Ngati ndiwe wokondwa, pitirira chomwecho. Usadzachitenso konse chirichonse cholakwika, ngati icho. Ingopitirira. Ndicho chisomo cha Mulungu.

²⁵ Tsopano ine ndikufuna kupempheranso ife tisanalowe mu Mawu. Ndi angati ati adzandipempherere ine? Ine ndikungopita kuchokera ku msonkhano kupita ku msonkhano. Kodi inu mupemphera?

Inu mukudziwa, ine ndikufuna kukuyimbirani inu kanyimbo kakang'ono, tonse a ife palimodzi, ife tisanapite ku Mawu. Chabe ku...kotero kuti ife tidzadziwe Mulungu... Kudzipereka chabe pang'ono. Kodi inu munayimvapo nyimbo yaying'ono iyi, *Iye Asamalira Inu?* "Kupyola mu kuwala ndi zisoni, Iye asamalira inu."

²⁶ Dona wamng'ono amene akubwera ku limba. Nditi, ine ndikufuna kuthokoza dona wamng'ono uyu, nayenso. Ine sindinadziwe konse yemwe iye anali. Ndi mmodzi wa ana aakazi a madikoni kuno. Ine ndithudi...Msungwana wamng'ono wa M'bale Wheeler. Iye wakula tsopano. Iye anali kanthu kakang'ono kamene kankakhala pa bondo langa, osati kale litali, ndipo tsopano iye ndi mkazi wamng'ono. Kotero ine ndithudi ndikumuthokoza iye kuti iye wagwiritsa ntchito luso lake mu nyimbo, ndipo tsopano iye amayimba mokoma kwambiri. Kodi inu mungatipatse ife poyambira, mlongo? Tonse a ife palimodzi tsopano.

Iye asamala inu,
Iye asamala inu;
Mkuwala kapena mthunzi,
Iye asamala inu.

Inu mumayikonda iyo? Tiyeni tiyiyimbenso iyo, tonse palimodzi.

Iye asamala inu,
Iye asamala inu;
Mkuwala kapena mthunzi,
Iye asamala inu.

M'bale Dauch, Iye amatero kwa inu, nanunso, m'bale. Kodi inu simukumukonda Iye? [Osonkhana anena, "Ameni."—Mkonzi.]

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu tsopano.

²⁷ Okonedwa Mulungu Wachisomo, ndi cholemba chaching'ono ichi apa cha zinthu pang'ono zoti ndinene kwa anthu, ndi kubwereranso kufaniziranso kwa wa mmawa uwu, pakuti ndicho chimene anthu abwera kudzamva. Ine ndikupemphera, Mulungu kuti Inu mudzawalola anthu kuti awone kuti Mulungu amakonda ndi kusamalira. Ndipo sindinali ine amene anapereka Izo, Ambuye, izo zinatsimikiziridwa kuti icho chinali Choonadi. Kotero ine ndikupemphera, Wokonedwa Mulungu, kuti chikondi Chanu nthawizonse chidzatsalira pakati pa anthu. Usiku uno, kudzasiyana utatha msonkhano uwu ndi kupita kwathu kosiyana, izo—izo zimakhala ngati zimatikoka ife, kwina, kuya, Ambuye. Ine ndikupemphera kuti Inu mudzadalitse anthu awa.

²⁸ Tsopano pamene ife tikufika ku Mawu, mu pemphero, ndi tikufika ku Mawu olembedwa, ife tikupempha kuti Inu mudzatenga Mawu olembedwa awa ndi kuwapanga Iwo amoyo kwa ife usikuuno. Ndipo pamene ife tichoka mu nyumba yino usiku uno kusiyana kuti tizipita mmakwathu mosiyana, mulole ife tinene monga iwo amene ankachokera ku Emausi, amene anali atayenda naye Iye tsiku lonse ndipo sanamudziwebe Iye; koma pamene Iye anawatengera iwo mkati mwa chipinda usiku uja, ndipo zitseko zonse zitatsekedwa, Iye anachita chinachake monga ngati Iye anachitira chisanachitike chipachikiko Chake. Ndi izo, iwo anadziwa kuti Iye anali atawukanso.

Chitani izo kachiwiri usiku uno, Ambuye. Perekani izo, pamene zitseko zatsekedwa, ndipo gulu Lanu laling'ono apa lakhala, likudikira. Ndipo, Atate, pamene ife tidzapita mmakwathu, ife tidzanena monga iwo anachitira, "Kodi mitima yathu siyinatenthe mkati mwathu pamene Iye amalankhula kwa ife motsatira njira!" Ife tikudzipereka tokha, ndi tonse, m'manja Mwanu, Ambuye. Muchite ndi ife pamene Inu muwona kuyenera. Mu Dzina la Yesu. Ameni.

²⁹ Tsopano tiyeni ife tilowe kumene mu utumiki tsopano, mwamsanga. Kutembenuza tsopano ndi ine, ngati inu mungathe, ku Bukhu la Ahebri, ndi vumbulutso lina pa Uthenga. Ife tidzalankhula kwa mphindi pang'ono chabe usiku uno, Ambuye akalola. Ndiyeno pamene tikuwerenga ndime zoyamba zitanu za Ahebri 7:1 mpaka 3, ndiyeno kuchitira ndemanga pa izi. Ndipo ife sitikudziwa chimene Ambuye ati achite; ife sitikudziwa. Chinthu chokha chimene ife tikuchita chiri kungokhulupirira, kuyang'anira, kupemphera. Nkulondola uko? Ndi kukhulupirira kuti "Iye apanga chirichonse kugwira ntchito palimodzi kwa

ubwino kwa iwo amene amamukonda Iye,” chifukwa Iye analonjeza kutero.

Pakuti Melkizedeki uyu, mfumu ya Salemu, wansembe wa Mulungu wammwambamwamba, amene anakomana naye Abrahamu akubwerera kuchokera kokapha mafumu, namudalitsa iye;

Kwa iyenso Abrahamu anamupatsa gawo la khumi la zonse; poyamba pokhala mwakumasulira Mfumu ya chirungamo, ndipo zitatha izo naponso Mfumu ya Salemu, amene ali, Mfumu ya Mtendere;

Tiyeni tiwerenge mopitirira pang’ono.

Wopanda bambo, wopanda mayi, wopanda kholo, . . . ngakhale chiyambi cha masiku, kapena mathero a moyo; koma anapangidwa ngati Mwana wa Mulungu; akhala wansembe mopitiriza.

³⁰ Taganizani za Munthu wamkulu uyu, wamkulu chotani Munthu uyu ayenera kuti anali! Ndipo tsopano, funso liri, “Ndi ndani Munthu uyu?” Azaumulungu akhala nawo malingaliro osiyana. Koma kuyambira chitsegulireni cha Zisindikizo Zisanu ndi ziwiri, Bukhu lachinsinsi limene lakhala lachinsinsi kwa ife. . . Molingana ndi Chivumbulutso 10:1 mpaka 7, zinsinsi zonse zimene zalembedwa mu Bukhu ili, zimene zakhala zitabisika konse kupyola mu m’badwo wa okonzanso, ziyenera kubweretsedwa powonekera ndi mngelo wa m’badwo wa mpingo wotsiriza. Ndi angati akudziwa kuti izo nzolondola? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Uko nkulondola, ziyenera kubweretsedwa. Zinsinsi zonse za Bukhu lachinsinsi ziri zoti zidzaululidwa kwa mtumiki wa Laodikaya wa m’badwo umenewo.

³¹ Powona kuti pali kutsutsana kochulukana za Munthu uyu ndi phunziro ili, ine ndikuganiza icho chikutikakamiza ife kulowa mu izo, kuti tipeze Yemwe uyu ali. Tsopano, alipo masukulu angapo a lingaliro pa Iye.

Imodzi ya masukulu ili, imati, “Iye ali nthano chabe. Iye sanali munthu kwenikweni.”

Ndipo ena amanena, kuti, “Iwo unali unsembe, uwo unali unsembe wa Melkizedeki.” Ndiyo ili yodziwika kwambiri, yomwe imagwira bwino kumbali iyo kuposa momwe iwo amachitira kwa yina, ndi chifukwa iwo amanena kuti iwo unali unsembe.

Izo sizingakhoze kukhala zimenezo, pakuti mu mutu wa 4 Iwo akunena kuti Iye anali Munthu, “Mwamuna.” Kotero, kuti akhale Munthu, Iye ayenera kukhala nawo umunthu, “Mwamuna.” Osati dongosolo; koma Munthu! Kotero Iye sanali chabe dongosolo la unsembe, ngakhalenso kuti Iye anali nthano. Iye anali Munthu.

³² Ndipo Munthuyo ali Wamuyaya. Ngati inu mungazindikire, “Iye analibe bambo. Iye analibe mayi. Iye analibe nthawi imene Iye anayamba konse. Ndipo Iye analibe nthawi imene Iye anatherapo.” Ndipo yense Yemwe iye anali akadali wamoyo usikuuno, chifukwa Baibulo linanena apa, kuti, “Iye analibe ngakhale bambo, kapena amayi, chiyambi cha masiku, kapena mathero a moyo. Kotero Iye anayenera kukhala Munthu Wamuyaya. Nkulondola uko? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Munthu Wamuyaya! Kotero iye akanakhoza kokha kukhala Munthu mmodzi, ndiye Mulungu, chifukwa Iye ali Mmodzi yekhayo amene ali Wamuyaya. Mulungu!

³³ Tsopano, mu Timoteo Woyamba 6:15 ndi 16, ngati inu mukufuna kuwerenga izo nthawiyina, ine ndikufuna kuti inu muwerenge izo.

Tsopano, chinthu chimene ine ndikumenyera chiri, kuti, Iye anali Mulungu, chifukwa Iye ali Munthu yekhayo amene angakhoze kukhala wachisavundi. Ndipo tsopano, Mulungu kudzisintha Iyemwini mwa Munthu; ndicho chimene Iye anali, “Wopanda bambo, wopanda mayi, wopanda chiyambi cha moyo, wopanda mathero a masiku.”

³⁴ Tsopano ife tikupeza mu Lemba kuti anthu ambiri amaphunzitsa kuti, “umunthu utatu mu Umulungu.” Kotero, inu simungakhoze kukhala nawo umunthu popanda kukhala munthu. Zimatengera munthu kuti apange umunthu.

Mtumiki wa Baptisti, masabata pang’ono apitawo, anabwera, ndipo ku nyumba yanga, ndipo anati, “Ine ndikufuna kudzakuwongola iwe pa Umulungu nthawiyina pamene iwe udzakhale nayo nthawi.” Anandiyitana ine, kani.

³⁵ Ine ndinati, “Ine ndiri nayo nthawi pakali pano, chifukwa ine ndikufuna kuwongoka, ndipo ife tinayika kumbali china chirichonse, kuti tichite icho.”

Ndipo iye anadza, iye anati, “M’bale Branham, inu mumaphunzitsa kuti pali Mulungu mmodzi chabe.”

Ine ndinati, “Inde, bwana.”

Iye anati, “Chabwino,” iye anati, “Ine ndikukhulupirira kuti pali Mulungu mmodzi, koma Mulungu mmodzi mwa Anthu atatu.”

Ine ndinati, “Bwana, bwerezaninso izo.”

Iye anati, “Mulungu mmodzi, mwa Anthu atatu.”

³⁶ Ine ndinati, “Inu munapita ku sukulu yakuti?” Mukuona? Ndipo iye anandiuza ine b—Baibulo koleji. Ine ndinati, “Ine ndikhoza kukhulupirira izo. Iwe sungakhoze kukhala munthu wopanda kukhala umunthu. Ndipo ngati ndiwe umunthu, ndiwe umunthu umodzi kwa iwemwini. Ndiwe wapadera, munthu mmodzi payekha.”

Ndipo iye anati, “Chabwino, azaumulungu sangakhoze ngakhale kufotokoza izo.”

Ine ndinati, “Ziri mwa vumbulutso.”

Ndipo iye anati, “Ine sindingakhoze kuvomereza vumbulutso.”

³⁷ Ine ndinati, “Ndiye palibe njira yomwe Mulungu angafikire konse kwa inu, chifukwa, ‘Izo zinabisika ku maso a anzeru ndi aluntha, ndi kuwululidwa kwa makanda,’ kuwululidwa, vumbulutso, ‘kuwululidwa kwa makanda onga amene ati adzavomereze izo, kuphunzira.’” Ndipo ine ndinati, “Sipadzakhala njira yomwe Mulungu kuti afikire kwa inu; inu mukudzitseka nokha kwa Iye.”

Baibulo lonse liri vumbulutso la Mulungu. Mpingo wonse wamangidwa pa vumbulutso la Mulungu. Palibe njira yina yomodziwira Mulungu, kokha mwa vumbulutso. “Kwa iye amene Mwana ati adzamuwululire Iye.” Vumbulutso; chirichonse chiri vumbulutso. Kotero, kula...Kusalandira vumbulutso, ndiye ndiwe wazaumulungu wozizira basi, ndipo palibe chiyembekezo kwa iwe.

³⁸ Tsopano, tsopano, ife tikupeza kuti Munthu uyu “analibe bambo, wopanda mayi, wopanda chiyambi cha masiku kapena mathero a moyo.” Anali Mulungu, *en morphe*.

Tsopano, dziko, mawu ochokera, mawu a Chigriki, amatanthawuza, “kusintha,” ankagwiritsidwa ntchito. Kudzisintha Iyemwini, *en morphe*, kuchokera kwa munthu mmodzi ku...Munthu mmodzi; mawu a Chigriki pamene, *en morphe*, amatanthauza...Iwo anatengedwa kuchokera ku sewero la pasiteji, limene munthu mmodzi akusintha chigoba chake, kuti zimupange iye khalidwe lina.

³⁹ Monga mu—mu sukulu, posachedwa kumene, ine ndikukhulupirira, Rebekah, asanatsirize kumene sukulu, iwo anali nalo limodzi la sewero la Shakespeare. Ndipo mnyamata mmodzi amachita kusintha zovala zake nthawi zingapo, chifukwa iye ankawewera magawo awiri kapena atatu osiyana; koma, munthu yemweyo. Iye anatuluka, nthawi imodzi, iye anali mthakati; ndipo pamene iye anatuluka nthawi yotsatira, iye anali khalidwe lina. Ndipo tsopano mawu a Chigriki, *en morphe*, amatanthawuza kuti iye “anasintha chigoba chake.”

⁴⁰ Ndipo ndicho chimene Mulungu anachita. Ali Mulungu yemweyo nthawi zonse. Mulungu mmawonekedwe a Atate, m—Mzimu, Lawi la Moto. Mulungu yemweyo anapangidwa thupi nakhala pakati pathu, *en morphe*, anatulukira kotero kuti Iye akhoze kuwonedwa. Ndipo tsopano Mulungu yemweyo ali Mzimu Woyera. Atate, Mwana, Woyera... osati Amulungu atatu; mauidindo atatu, machitidwe atatu a Mulungu mmodzi.

⁴¹ Baibulo linati, “Pali Mulungu mmodzi,” osati atatu. Koma ndimo mwemo iwo sangakhoze . . . Inu simungakhoze kuwongola izi ndi kukhala nawo Amulungu atatu. Inu simungamugulitse Myuda izo. Ine ndikuuzani inu izo. Mmodzi yemwe amadziwa bwino, iye amadziwa kuti pali Mulungu mmodzi yekha.

⁴² Zindikirani, monga wosema, iye amabisala, ndi—chigoba pa iye. Ndicho chimene Mulungu wachita kwa m’badwo uno. Izo zabisika. Zinthu zonse izi zabisika, ndipo zikuyenera kuwululidwa mu m’badwo uno. Tsopano, Baibulo limanena kuti izo zidzawululidwa mu nthawi zamtsogolo. Ziri ngati wosema kusunga yake—chidutswa cha ntchito yake chonse chophibidwa mpaka nthawi imene iye achotsa chigoba cha icho ndipo apo icho chiri.

Ndipo ndicho chimene Baibulo lakhala liri. Iyo yakhala ntchito ya Mulungu imene yaphimbidwa. Ndipo Izo zabisika chikhazikitsireni maziko a dziko, ndipo Ndicho chinsinsi chofutukuka pasanu ndi pawiri. Ndipo Mulungu analonjeza mu tsiku ili, pa m’badwo wa mpingo wa Laodikaya uwu, kuti Iye adzachotsa chigoba kwa chinthu chonsecho ndipo ife tikhoza kuchiwona Icho. Ndi chinthu chaulemerero bwanji!

⁴³ Mulungu, *en morphe*, anaphimbidwa mu Lawi la Moto. Mulungu, *en morphe*, mwa Munthu wotchewda Yesu. Mulungu, *en morphe*, mu Mpingo Wake. Mulungu pamwamba pathu, Mulungu nafe, Mulungu mwa ife; kudzichepetsa kwa Mulungu.

Pamwamba Apo, woyera, palibe mmodzi akanakhoza kumukhudza Iye, Iye anakhala pa phiri; ndipo ngakhale ngati chinyama chikanakhudza phirilo, chikanafa.

Ndiyeno Mulungu anabwera pansu ndi kusintha hema Yake, ndipo anabwera pansu nakhala nafe ife, kukhala mmodzi wa ife. “Ndipo ife tinamugwira Iye,” Baibulo linatero. Timoteo Woyamba 3:16, “Popanda kutsutsana chinsinsi cha umulungu nchachikulu; pakuti Mulungu anawonetseredwa mu thupi, anagwiridwa ndi manja.” Mulungu kudya nyama. Mulungu anamwa madzi. Mulungu anagona. Mulungu analira. Iye anali mmodzi wa ife. Mokongola, kuyimiridwa mu Baibulo!

Uyo anali Mulungu pamwamba pathu; Mulungu nafe; tsopano ndi Mulungu mwa ife, Mzimu Woyera. Osati Munthu wachitatu; Munthu yemweyo!

⁴⁴ Mulungu anabwera pansu ndi kukhala thupi, ndipo anafa imfa, mwa Khristu; kotero kuti Iye akakhoze kuyeretsa Mpingo, polinga kuti alowe mwa iwo, kufuna chiyanjano. Mulungu amakonda chiyanjano. Ndicho chimene Iye anamupangira munthu pa nthawi yoyamba, chinali chifukwa cha chiyanjano; Mulungu amakhala yekha, ndi akerubi.

⁴⁵ Ndipo zindikirani tsopano, Iye anapanga munthu, ndipo munthu anagwa. Kotero Iye anabwera pansu namuwombola munthu, chifukwa Mulungu amakonda kupembedzedwa.

Mawu omwewo akuti *mulungu* amatanthawuza “chinthu chopembedzedwa.”

Ndipo ichi chimene chimabwera pakati pathu, ngati Lawi la Moto, ngati chinachake chimene chimasintha mitima yathu, ameneyo ali Mulungu yemweyo amene anati, “Apo pakhale kuwala,” ndipo panali kuwala. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwa nthawizonse.

⁴⁶ Tsopano, pachiyambi Mulungu ankakhala yekha, ndi zokhumba Zake, monga ine ndinalankhulira mmawa uno. Ndiwo malingaliro Ake. Panalibe kanthu, Mulungu yekha basi, koma Iye anali nawo malingaliro.

Monga ngati womanga wamkulu akhoza kukhala pansi, mmaganizo mwake, najambula zimene iye akuganiza ndizo iye akupita ku—kukamanga. Kulenga, tsopano, iye sangakhoze kulenga. Iye akhoza kutenga chinachake chimene chalengedwa ndi kuchipanga icho mmawonekedwe osiyana; chifukwa Mulungu ali njira yokhayo. . . Mmodzi yekhayo amene akhoza kulenga. Koma iye amatenga mmaganizo mwake zimene iye ati achite, ndipo ndiwo malingaliro ake, ndizo zokhumba zake. Tsopano ndilo lingaliro, ndiyeno iye amalinyankhula ilo, ndipo ndiwo mawu ndiye. Ndipo m—mawu ali. . .

⁴⁷ Lingaliro, pamene ilo lifotokozedwa, liri mawu. Lingaliro lofotokozedwa liri mawu, koma ilo liyenera kukhala lingaliro poyamba. Koteru, ndizo zikhumbo za Mulungu; ndiye izo zimadzakhala lingaliro, kenako mawu.

⁴⁸ Zindikirani. Iwo amene ali nawo, usikuuno, Moyo Wamuyaya, anali naye Iye ndi mwa Iye, mu kuganiza Kwake, pasanakhale konse Mngelo, nyenyezi, Mkerubi, kapena china chirichonse. Ndiwo Umuyaya. Ndipo ngati inu muli nawo Moyo Wamuyaya, inu nthawizonse munalipo. Osati umunthu wanu apa, koma thunthu ndi mawonekedwe amene Mulungu wopanda malire. . .

⁴⁹ Ndipo ngati Iye sali wopanda malire, Iye sali Mulungu. Mulungu ayenera kukhala wopanda malire. Iye tiri nawo malire; Iye ali wopanda malire. Ndipo Iye anali wopezekapaliponse, wodziwazonse, ndi wamphamvuzonse. Ngati Iye sali, ndiye Iye sangakhoze kukhala Mulungu. Amadziwa zinthu zonse, malo onse, chifukwa cha kupezekapaliponse Kwache. Kudziwazonse kumamupangitsa Iye kupezekapaliponse. Iye ali Umunthu; Iye sali ngati mphepo. Iye ali Umunthu; Iye amakhala mu nyumba. Koma pokhala wodziwazonse, kudziwa zinthu zonse, kumamupangitsa Iye wopezekapaliponse, chifukwa Iye amadziwa chirichonse chimene chikuchitika.

Sipangakhoze kukhala nyerere yophethira maso ake koma imene Iye akuyidziwa. Ndipo Iye anadziwa iyo pasanakhale dziko, nthawi yochuluka chotani iyo iti idzaphethire maso ake, ndiponso kuchuluka kwa mafuta amene iyo inali nawo mwa

iyo, pasanakhale konse dziko. Uko ndi kusakhala nawo malire. Ife sitingakhoze kumvetsa izo mmaganizo mwathu, koma ndizo Mulungu. Mulungu, wopanda malire!

⁵⁰ Ndipo kumbukirani, inu, maso anu, thunthu lanu, chirichonse chimene inu munali, inu munali mu kuganiza Kwake pachiyambi. Ndipo chinthu chokhacho chimene inu muli chiri chifotokozo, mawu. Atatha Iye kulingalira iwo, Iye anawalankhula iwo, ndipo ndinu apa. Ngati izo siziri, ngati inu simunali mu maganizo Ake, palibe njira nkomwe yomwe inu mungakakhalire kumeneko, pakuti Iye ali Mmodzi amene amapereka Moyo Wamuyaya.

⁵¹ Inu mukukumbukira momwe ife tinawerengera Malemba? “Osati iye amene afuna, kapena iye amene athamanga, koma Mulungu!” Ndipo kuti kukonzeratu Kwache kuyime moona, Iye akanakhoza kusankha, isanakwane nthawi iliyonse, ndani. Mulungu ali wochita mwayekha mu kusankha Kwache. Kodi inu mumadziwa izo? Mulungu ali wochita mwayekha.

Ndindani amene analipo kumbuyo uko kuti amuwuze Iye njira yabwino yopangira dziko? Ndani angayerekeze kumuwuza Iye kuti Iye anali kuyendetsa ntchito Yake molakwika?

Ngakhale amene—Mawu amene, Iwoeni, kuchita mwa iwo wokha kwambiri. Ngakhale vumbulutso liri lochita mwa lokha. “Iye amavumbulutsa kwa amene Iye ati amuwululire.” Vumbulutso limene, iloleni, liri lochita mwa lokha mwa Mulungu. Ndimomomwe anthu amapondera pa zinthu, nalumphap pa zinthu, nagunda pa zinthu, osadziwa chimene iwo akuchita. Mulungu ali wochita mwayekha mu ntchito Zake.

⁵² Tsopano ife tikumupeza Iye pachiyambi, zokhumba Zake. Ndipo, tsopano, inu munali naye Iye pamenepo. Pamenepo ndi pamene Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa mu kuwonekera.

Tsopano, ife tikuwerenga cha apa mu Chivumbulutso mutu wa 13, ndime ya 8, kuti, “Chirombo chimene chikubwera pa dziko lapansi,” mu masiku otsiriza awa, “Chidzanyenga anthu onse awo pa dziko lapansi amene mayina awo sanalembedwe mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko a dziko asanakhalepo.”

⁵³ Taganizani za izo! Yesu asanabadwe nkomwe, zaka zikwi zinayi Iye asanadze pa dziko lapansi, ndi zaka zikwi zambiri inu musanadze pa dziko lapansi; Yesu, m’maganizo a Mulungu, anafera machimo adziko, ndipo Bukhu la Moyo linapangidwa, ndipo dzina lanu linayikidwa pa Bukhu la Moyo ilo maziko a dziko asanayikidwe. Ndicho Choonadi cha Baibulo. Onani, dzina lanu linakonzedweratu ndi Mulungu ndi kuyikidwa pa Bukhu la Moyo maziko a dziko asanayikidwe.

⁵⁴ Inu munali mmenemo mu zokhumba Zake. Inu simukukumbukira izo, ayi, chifukwa ndinu chabe gawo la

Moyo Wake. Ndinu gawo la Mulungu pamene inu mukhala mwana wamwamuna kapena mwana wamkazi wa Mulungu.

Basi monga inu muli gawo la atate anu apadziko lapansi! Ndiko kulondola. Inu muli. Wamphongo amanyamula magazi anu moyo, magazi. Ndipo pamene iwo alowa mu—mu dzira, ndiye inu mumakhala gawo la abambo anu; ndipo amayi anu ali gawo la abambo anu, nawonso; kotero ndinu nonse gawo la abambo anu.

Ulemerero! Izo zimatulutsa zipembedzo kunja, palimodzi. U-nhu. Ndithudi zimatero! Mulungu, mu zonse, malo okhawo!

⁵⁵ Zindikirani tsopano chikhumbo Chake. Ndiye chikhumbo chinali, choyamba, Mulungu; lingaliro, chikhumbo pachokha, zonse mu Chimodzi, popanda kufotokozedwa. Ndiye pamene Iye anafotokoza, mwachiwiri, Iye anakhala ndiye Mawu. “Ndiyeno Mawu anapangidwa thupi nakhala pakati pathu.”

⁵⁶ Yohane Woyera mutu wa 1 ndi ndime ya 1, zindikirani, izi ziri, “Pachiyambi.” Koma, pasanakhale, Wamuyaya! Zindikirani, “Pachiyambi panali Mawu.” Pamene nthawi inayamba, iwo anali Mawu. Koma iwo asanakhale Mawu, icho chinali chikhumbo, lingaliro. Ndiye ilo linafotokozedwa, “Pachiyambi panali,” chifotokoza, “Mawu.”

Tsopano ife tikufika kumene Melkizedeki ali. Ndiye Munthu wachinsinsi uyu. “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu.” “Ndiyeno Mawu anakhala thupi nakhala pakati pathu.” Gwirani izo apo tsopano, zindikirani.

⁵⁷ U—umunthu Wake woyamba unali Mzimu, Mulungu, wauzimu, chabwino, Wamuyaya wamkulu. Chachiwiri, Iye anayamba kudzipanga Iyemwini kumka ku thupi, mu *fiofane*, ilo limatchedwa “Mawu; thupi.” Umu ndiye momwe Iye analiri pamene Iye anakomana naye Abrahamu, ankatchedwa Melkizedeki. Iye anali mu mawonekedwe a fiofane. Tsopano ife tidzafika kwa izo ndi kutsimikizira izo mu maminiti pang’ono, Ambuye akalola. Iye anali Mawu.

⁵⁸ Fiofane ndi chinachake chimene iwe sungakhoze kuchiwona. Icho chikhoza kukhala pomwe apa tsopano, komabe iwe sungakhoze kuchiwona icho.

Ndizo monga ngati, chabwino, ngati televizioni. Izo ziri mu dera lina. Televizioni; anthu akusuntha kumene kupyola mu chipinda ichi tsopano, akuyimba; pali mitundu, nayonso. Koma diso liri kokha lomvera ku mphamvu zisanu. . . Umunthu wanu wonse uli kokha womvera ku mphamvu zisanu, kani. Ndipo inu muli kokha womvera ku zomwe kupenya kwapatsidwa kuti kupenye. Koma pali dera lina lomwe likhoza kuwonedwa mwa kusinthidwa, ndi televizioni.

⁵⁹ Tsopano, televizioni siyimapanga chithunzi. Televizioni imawongolera kokha icho mu njira, ndiyeno kanema wa Televizioni amatenga icho. Koma chithunzi chiri pamenepo, kuyamba ndi kuyamba. Televizioni inalipo pano pamene Adamu anali pano. Televizioni inalipo pano pamene Eliya anakhala pa phiri la Karimeli. Televizioni inalipo pano pamene Yesu wa ku Nazareti anayenda magombe a Galileya. Koma inu mukungozipeza kumene izo tsopano. Iwo sakanakhulupirira izo kumbuyo uko. Iwe ukanakhala wamisala kuti unene chinachake ngati icho. Koma tsopano izo zakhala chenicheni.

Ndipo kotero izo ziri, kuti Khristu ali pano, Angelo a Mulungu ali pano. Ndipo tsiku lina, mu Zakachikwi zazikulu zakudza, izo zidzakhala basi zenizeni kochulukira kuposa televizioni kapena china chirichonse, chifukwa izo ziri pano.

⁶⁰ Iye akudziwulula Iyemwini mu mawonekedwe Ake akulu a chimene Iye ankadzinenera, pamene Iye *adzisinthira* Iyemwini mwa antchito Ake nadzitsimikizira Iyemwini.

⁶¹ Tsopano, apa Iye ali mu mawonekedwe a Mzimu. Ndiyeno Iye anadza mmawonekedwe a . . . a *kudzisinthira*. Tsopano, Iye anawonekera kwa Abrahamu, *en morphe*. Pamene Abrahamu anali kubwerera kokapha mafumu, apa pakudza Melkizedeki, analankhula naye Iye.

⁶² Tsiku lina mu pepala ya ku Tucson, ine ndinali kuwerenga nkhani imene pamene panali m—mkazi akuyendetsa mu msewu, ine ndikukhulupirira pafupi makumi anayi, mailosi makumi asanu pa ora, ndipo iye anagunda munthu wokalamba atavala chikhoto. Iye anafuula nayimitsa galimoto lake. Iyo inamuponyera iye mmwamba. Komwe ku chipululu chasee! Ndipo iye anathamangira mmbuyo kuti akamupeze iye, ndipo iye panalibe pamenepo. Kotero kodi iye anachita chiani? Anthu ena kumbuyo kwake anawona izo zikuchitika, anamuwona bambo wamkuluyo akuwuluka mmwamba, ndi chikhoto chake chikutembenezika. Kotero iwo anathamangira mmbuyo kuti akafufuze. Iwo sanakhoze kumupeza munthuyo paliponse. Iwo anayitana apolisi. Apolisi anabwera kudzayesa malowo; panalibe aliyense pamenepo.

⁶³ Chabwino, wina aliyense wa iwo anachitira umboni kuti, “Galimoto inathamanga, niyigunda munthuyo. Iye anapita mmwamba mu mlengalenga, ndipo aliyense anayiwona iyo.” Mboni, ndipo magalimoto awiri kapena atatu akatundu a iwo, iwo anaziwona izo zikuchitika. Anadzapeza kuti, zaka zisanu zapitazo, panali munthu wokalamba atavala chikhoto, anagundidwa ndi kuphedwa pa malo omwewo.

Pamene inu muchoka kuno, inu simunafe. Inu mudzayenera kubwereranso, ngakhale ngati muli wochimwa, ndi kuwerezidwa molingana ndi ntchito zochitidwa mu thupi.

“Ngati kachisi wa dziko lapansi uyu asungunuka, ife tiri naye wina akuyembekezera.” *En morphe*, ndiwo mawu.

⁶⁴ Tsopano, Mulungu, mu siteji iyi ya...Ndi siteji ya chirengedwe Chake, kenako anapangidwa mu thupi, Yesu. Kuchokera ku chiyani? Kuchokera ku chiyambi chachikulu, Mzimu, ndiye anabwera pansu kudzakhala Mawu, kudzitulutsa Iyemwini kunja. Mawu sakudzipangabe Wokha, iwo anangolankhulidwa, *en morphe*, kenako Iye akukhala thupi, Yesu, chivundi, kuti atilawire imfa ife tonse ochimwa.

⁶⁵ Pamene Abrahamu anakomana naye Iye, Iye anali Melkizedeki. Iye akufutukula apa zimene zikhumbo zonse ziti zidzachte mu kutsiriza kwa mathero, mwana aliyense wa Abrahamu. Mwana aliyense wa Chikhulupiro adzachita mwamtheradi chinthu chomwecho. Koma ine ndikufuna kupenya momwe ife tiyenera kubwerera.

⁶⁶ Ndiponso, ife tikumuwona Iye akuwululidwa apa mwa Rute ndi—ndi Boazi, ngati Wowombola Wachibale, momwe Iye anachita kubwera kudzakhala thupi.

⁶⁷ Tsopano ife tikuona chikhumbo, ana a Mzimu Wake, sanalowebe mu thupi la mawonekedwe—a Mawu. Koma, fiofane; thupi ili liri lomvera ku Mawu ndi chikole, kuyembekezera chikole, kusintha kwa thupi.

⁶⁸ Tsopano, kusiyana kwa pakati pa Iye ndi inu, ngati mwana. Onani, Iye anali, pachiyambi, Mawu, thupi la *en morphe*. Iye anadza mkati nakhala mmenemo, mwa Munthu wa Melkizedeki. Ndiye, kenako, ife sitinamvenso za Melkizedeki, chifukwa Iye anadzakhala Yesu Khristu. Melkizedeki anali Wansembe, koma Iye anadzakhala Yesu Khristu. Tsopano, inu munalidutsa ilo. Chifukwa, mmawonekedwe awo, Iye ankadziwa zinthu zonse, ndipo inu simunakhozebe kudziwa izo.

Inu munabwera ngati Adamu, ngati ine, inu munakhala kuchokera ku chikhumbo kukhala thupi, kuti mudzayesedwe. Koma pamene moyo uwu watha kuno, “Ngati msasa wa dziko lapansi ukhala utasungunuka, ife tiri nawo wina ukuyembekezera.” Ndiko kumene ife timapita; awo ali Mawu. Ndiye ife tikhoza kuyang’ana mmbuyo ndikuwona zimene ife tachita. Tsopano ife sitikumvetsa izo. Ife sitinakhalebe Mawu; ife tangokhala chabe munthu-wathupi, osati Mawu.

⁶⁹ Koma, ndipo penyani, mowonekera zimapangitsa izo kuwoneka, inu simudzakhala konse Mawu kokha ngati inu munali lingaliro pachiyambi. Izo zikutsimikizira kukonzeratu kwa Mulungu. Mwaona? Inu simungakhoze kukhala Mawu kokha ngati muli lingaliro. Inu munayenera kukhala mu kuganiza, poyamba.

Koma, inu mukuona, kuti mugonjetse kuyesedwa, inu munachita kulambalala fiofane. Inu munachita kubwera pansu pano mu thupi, kuti mudzayesedwe ndi tchimo. Ndiyeno, ngati

inu muyima, “Onse amene Atate andipatsa Ine adzadza kwa Ine, ndipo Ine ndidzamuwukitsa iye pa masiku otsiriza.” Onani, inu munkayenera kukhala poyamba.

⁷⁰ Ndiyeno, inu mukuona, Iye anabwera pansi pomwe, mzere wa nthawizonse, kuchokera ku chikhumbo kupita. . . Maziko a dziko asanakhale, dzina lake layikidwa pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Ndiye, kuchokera ku icho, Iye akukhala Mawu, fiofane, imene ikhoza kuwonekera, kusowa. Ndiyeno Iye akukhala thupi nabwereranso kachiwiri, kuwukitsa thupi lomwelo mu chikhalidwe cha ulemerero.

Koma inu munalambalala fiofane ndi kudzakhala munthu-wathupi, kuti muyesedwe ndi tchimo. Ndiyeno, “Ngati msasa wadziko lapansi uwu utha, ife tiri nawo wina ukuyembekezera kale.” Ife tikanalibe matupi.

⁷¹ Koma, taonani! Pamene thupi ili lilandira Mzimu wa Mulungu, Moyo wachisavundi mkati mwa inu, iwo umaponyera thupi ili mu kumvera kwa Mulungu. Aleluya! “Iye amene ali wobadwa wa Mulungu sachita tchimo; iye sangakhoze kuchimwa.” Aroma 8:1, “Palibe chotero chitsutso kwa iwo amene ali mwa Khristu Yesu; iwo samayenda monga mwathupi, koma mwa Mzimu.” Ndi zimenezotu. Onani, izo zimaponyera thupi lanu ku kumvera.

Inu simusowa kunena, “O, ngati ine nditangosiya kumwa! Ngati ine ndikanakhoza chabe. . .” Kungolowa mwa Khristu, ndipo zonse zapita, onani, onani, chifukwa thupi lanu liri lomvera kwa Mzimu. Ilo silirinso konse lomvera kwa zinthu zamdziko; izo ziri zakufa. Izo nzakufa; machimo anu akwiliridwa mu ubatizo, ndipo ndinu chirengedwe chatsopano mwa Khristu. Ndipo thupi lanu, kukhala lomvera kwa Mzimu, kuyesa kukhala moyo wa mtundu wolondola.

⁷² Monga inu akazi kumadzinenera kuti inu muli nawo Mzimu Woyera, ndi kumapita kunjira kuno ndi kumavala akabudula ndi zinthu, inu mungakhoze bwanji kuchita izo? Ungakhoze bwanji Mzimu wa Mulungu mwa inu kukulolani inu kuti muchite chinthu chotero? Sizingakhoze basi kukhala choncho. Ndithudi, izo sizingakhoze kukhala. Iye sali mzimu wauve; Iye ali Mzimu woyera.

⁷³ Ndiyeno pamene inu mukhala omvera kwa Mzimu umenewo, iwo umaponyera umunthu wanu wonse ku kumvera kwa Mzimu umenewo. Ndipo Mzimu uwo suli kanthu mu dziko koma Mawu a Mbewu awa akuwonetseredwa, kapena kufulumizitsidwa, aleluya, kupangidwa amoyo. Ndipo pamene Baibulo linati, “Musati muchite *ichi*,” thupi ilo mwamsanga limatembenukira kwa Ilo. Palibe funso.

Ndipo ndi chiyani icho? Ndicho chikole cha chiwukitsiro. Thupi ili lidzawukitsidwanso, chifukwa ilo layamba kale. Ilo linakhalapo nthawiyina lomvera kwa tchimo, ndi matope ndi

chivundi, koma tsopano ilo liri nacho chikole; ilo latembenukira Mwakumwamba. Tsopano, ndicho chikole kuti inu mukupita mu Mkwatulo. Ndicho chikole.

⁷⁴ Munthu wodwala atagona, akufa, wopanda chotsalira koma imfa; ndizo zokha zimene zikhoza kuchitika. Ine ndawonapo mithunzi ya anthu, itadyedwa ndi khansala ndi chifuwa chachikulu; ndi kuwawona anthu awo, kanthawi pang'ono zitatha izo, olunga mwangwiro ndi amphamvu. Ngati palibe machiritso Auzimu, ndiye palibe chiwukitsiro, chifukwa machiritso Auzimu ali chikole cha chiwukitsiro. Ameni!

⁷⁵ Inu mukudziwa chimene ndalama za chikole ziri, sichoncho inu? Ndizo malipiro apang'ono. "Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu; ndi mikwingwirima Yake ife tachiritsidwa." Zindikirani kudabwitsa kwache! Ife timamukonda Iye.

⁷⁶ Tsopano, thupi ili liri lomvera kwa Mzimu. Sitalowebe mu mawonekedwe a Mawu, koma ife tikadali mu mawonekedwe a thupi, koma omvera ku Mawu. Imfa mu thupi idzatitengera ife kumeneko.

⁷⁷ Chinthu chomwecho basi, taganizani za mwana wamng'ono. Inu mukhoza kumutenga mkazi, ziribe kanthu kaya iye ali woyipa chotani, pamene iye ali ndi pakati ndipo akukonzekera kukhala mayi. Yang'anani, mwana uyo asanabadwe, ine sindikusamala momwe mzimayi uyo aliri woyipa, iye amakhala wachifundo kwenikweni. Pali chinachake za kalankhulidwe kache. . . amawoneka waumulungu, kumuwona mayi wamng'ono akukonzekera kukhala mayi, ndi mwana. Chifukwa chiani izo? Thupi laling'ono ilo, tsopano, siliri la moyo apabe, onani, chinthu chokha chomwe ilo liri ndi mnofu chabe ndi akatumba. Kulumpha kwakung'ono uko, ndiwo akatumba basi amene akufufuma. Koma pamene ilo litulukira kuchokera ku chiberekeru, Mulungu amapumira mpweya wa moyo mwa ilo, ndiyeno iye amalira. Onani, basi ngati—ngati motsimikiza momwe paliri thupi lachibadwa limene likuwumbidwa, pali thupi lauzimu loti lilandire ilo mwamsanga pamene ilo lifika pano.

⁷⁸ Ndiye, pamene munthu abadwa kachiwiri, kuchokera Kumwamba, iye amadzakhala khanda la mzimu mwa Khristu.

Ndipo, ndiye, pamene mwinjiro wa thupi uwu lavulidwa, pali thupi lachibadwa, fiofane, thupi osati lopangidwa ndi manja, ngakhalenso kuti lobadwa mwa mkazi, limene ife timapitako.

Ndiye thupi ilo limabwereranso ndi kukatenga thupi la ulemerero.

Ndicho chifukwa Yesu anapita ku gehena pamene Iye anafa, nakalalikira ku miyoyo imene inali mu ndende; nabwerera kachiwiri mu fiofane uja. O, zododometsa! Tikuthokoza Mulungu!

⁷⁹ Akorinto Wachiwiri 5:1, “Ngati msasa wa dziko lapansi uwu ukhala utasungunuka, msasa wa dziko lapansi uwu, ife tiri nawo wina.” Onani, ife talilambalala ilo, kubwera molunjika kuchokera kwa Mulungu, chikhumbo; kuti tidzakhale mnofu, kuti tidzayesedwe ndi kuyesedwa ndi tchimo, monga Adamu anachitira. Koma pamene kuyesa kwa Mawu Ake kwatha, ndiye ife tikutengeredwa mmwamba ku thupi ili limene linakonzedwera ife maziko adziko asanakhale. Ali Mawu apo amene ife tinawalumphu, kubwera mozungulira kumene, pansi pano kuti tidzayesedwe ndi kuyesedwa. Ngati ife tikanabwera kupyola ilo, sipakanakhala yesero ayi; ife tikanadzadziwa zinthu zonse. Ndicho chifukwa Yesu ankadziwa zinthu zonse, chifukwa Iye anali Mawu Iye asanakhale thupi. Ndiye ife tikukhala Mawu.

⁸⁰ Apa ife tikuwumbidwa ku fanizo la Mawu, kuti tikhale otenga nawo Mawu, kudya pa Mawu, pokhala okonzedweratu kuchokera pachiyambi; inu mukuona kuyaka pang’ono uko kwa Moyo kumene inu munali nako kuchokera pachiyambi, pamene inu munayamba ulendo wanu. Ambiri a inu mukhoza kukumbukira izo. Inu munalowa mpingo *uwu* ndi kulowa mpingo *uwu*, inu munayesa *uwu* ndi *uwu*; palibe chimene chinakhutitsa. Uko nkulondola. Koma tsiku lina inu munangowazindikira Iwo. Kulondola.

⁸¹ Usiku wina ine ndinali kuphunzitsa kwinkakwake, ine ndikuganiza kuti kunali mu California kapena Arizona, za . . . Ine ndikukhulupirira ine ndanenapo kanthano kakang’onoka pano, za munthu kuyika nkhuku ndipo anali nalo dzira la mphungu pansu pa iyo. Ndipo pamene mphungu iyo inaswa, iye anali mbalame yosekesa-poyiwona imene nkhuku izo zinayiwonapo. Koma, iyo inkayenda pozungulira. Iyo inali—iyo inali yonyansa pakati pa izo, chifukwa iyo siyinkakhoza kumvetsa basi momwe nkhuku izi zinkalirira ndi kupalasa pa ndowe ndi kudya. Iye sankakhoza kumvetsa ganizolo. Nkhuku inkakhoza kunena, “Bwerani tidzadye, wokonedwa!” Koma, iye anali mphungu; iye samadya basi chotero. Icho sichinali chakudya chake.

⁸² Kotero iye amakhoza kugwira ziwala ndi zina, inu mukudziwa, ndi kuyitana tianapiye. Ndipo tianapiye tonse ito timakhoza kupita motsatira, kulira motsatira, nkudya. Koma mphungu yaying’ono siyinkakhoza chabe kuchita izo. Izo sizi—sizinkawoneka zabwino kwa iye.

Kotero tsiku lina amayi ake anabwera akumusaka iye.

⁸³ Ndipo iye amakhoza kuyimva nkhuku iyo ikulira. Iye amakhoza kuyesera mwakukhoza kwake kuti alire, koma iye sankakhoza kuchita izo. Iye anayesera kulira ngati nkhuku, koma iye sankakhoza kuchita izo. Onani, iye anali mphungu. Iye, kuyamba ndi kuyamba, iye anali mphungu. Iye anangofungatiridwa pansu pa nkhuku.

Ndizo ngati mamembala ena ampingo. Yense... Ndizo za momwe izo ziliri; za wina kunja kwa kakhazikitsidwe, ndi kulondola.

⁸⁴ Koma tsiku lina amayi ake anawuluka, ndipo iye anafuula. Iye anakuzindikira iko. Izo zinamveka molondola. Chifukwa chiani? Iye anali mphungu, kuyamba ndi kuyamba.

Ndimomwe izo ziliri ndi Uthenga, kapena Mawu, kapena Mphamvu ya Yesu Khristu. Pamene munthu wakonzedweratu ku Moyo Wamuyaya, iye amamva kuyimba koono uko, kufuula kwa Mulungu, palibe chimene chingamuletse iye kwa Iko.

Mpingo ukhoza kunena, “Masiku a chozizwitsa adutsa,” khulu, khulu, khulu. “Kuyima apa ndi kudya *izi*, ndi kuyima apa ndi kudya *izo*.”

⁸⁵ Zinthu za mkhola izo sizimuchitira iye, panonso. Iye wapita! “Zinthu zonse ndi zotheka!” Iye akunyamuka panthaka.

Ndicho chifukwa, vuto lake Akhristu ambiri lero, iwo sangakhoze kudzutsa phazi lawo kuchoka panthaka.

Mayi wakale anati, “Mwana, lumpha! Ndiwe mphungu. Bwera mmwamba muno kumene ine ndiri.”

Iye anati, “Mayi, ine sindinalumphepo, mu moyo wanga.”

⁸⁶ Iye anati, “Chabwino, iwe lumpha! Ndiwe mphungu, kuyamba ndi kuyamba. Sindiwe nkukhu.” Koteri iye anapanga kulumpaha kwache koyamba natambasula mapiko ake; sanachite bwino kwambiri, koma iye ananyamuka panthaka.

Ndimomwe ife timachitira. Ife timamuvomereza Mulungu mwa chikhulupiriro, mwa Mawu olembedwa. Pali chinachake mmenemo; ndiwo Moyo Wamuyaya uwo. Inu munakonzedweratu kwa iwo.

⁸⁷ Agogo ake aamuna ndi agogo ake aakazi anali mphungu. Iye anali mphungu, njira yonse mmbuyo. Mphungu sizimasakanizana ndi zinthu zina. Iye sali haiburidi, ayi. Iye ali mphungu.

⁸⁸ Ndiye, mutatha inu kuzindikira Mawu omwe a Mulungu kuti anali Chakudya cha Mphungu, ndiye iwe unasiya chinthu chinacho. Iwe uli ndiye kuwumbidwa mu fanizo lamoyo la Mulungu wamoyo. Iwe unamva kuchokera kwa fiofane yako. “Ngati thupi la padziko lapansi ili likhala litasungunuka, ife tiri nalo lina likuyembekezera.”

Inu mukuti, “Kodi ndi kulondola uko, M’bale Branham?”

Chabwino, tiyeni titenge mphungu ziwiri ndi kuyang’ana pa izo kwa maminiti pang’ono. Linalipo dzina, munthu wotchedwa Mose. Aliyense akudziwa kuti mneneri amatchedwa mphungu, mu Baibulo.

⁸⁹ Analipo mneneri wotchedwa Mose. Ndipo tsiku lina Mulungu anamuyitana iye, ndipo sanamulole iye kuti apite ku

dzikolo, ndipo iye—iye anafera pa thanthwe. Angelo anamutenga iye ndi kukamuyika iye.

Panali munthu wina, mphungu, sanasowe ngakhale kuti afe. Iye anangoyenda kuwoloka Yorodani, ndipo Mulungu anatsitsa gareta pansu; ndipo mwinjiro uwu wa thupi iye anawugwetsa, ndipo anakwera nakagwira mphoto ya nthawizonse.

Zaka mazana asanu ndi atatu kenako, zaka mazana asanu ndi atatu kenako, pa Phiri la Chiwalitsiro, apa panayima anthu awiri awo. Thupi la Mose linali litavunda kwa mazana a zaka, koma apa iye anali mu mawonekedwe otero mpaka ngakhale Petro, Yakobo, ndi Yohane anamuzindikira iye. Ameni! “Ngati msasa wa padziko lapansi uwu udzasungunuka,” ngati ndinu chikhumbo cha Mulungu chofotokozedwa pano pa dziko lapansi, “inu muli nalo thupi likuyembekeza pamene mudzachoka pa dziko lino.” Apo iwo analipo, atayima pa Phiri la Chiwalitsiro, mu fiofane yawo. Pakuti, iwo anali aneneri kwa amene Mawu anabwerako.

⁹⁰ Ndiponso tiyeni ife tizindikire mneneri wina, nthawi yina, wa dzina la Samuele. Iye anali munthu wamkulu. Iye anaphunzitsa Israeli; anawawuza iwo kuti asakhale naye mfumu. Iye anati, “Kodi ine ndinayamba ndanenapo kanthu kamodzi kwa inu mu Dzina la Ambuye kosati kamene kanachitika?”

Iwo anati, “Ayi. Chirichonse chimene inu munanena mu Dzina la Ambuye chinadzachitika.”

Iye anali mneneri, ndipo iye anafa.

⁹¹ Pafupi zaka zitatatu kapena zinai kenako, mfumu inakhala mu vuto; izo zinali Magazi a Yesu Khristu asanakhetsedwe nkomwe. Iye anali mu paradiso. Ndipo mfiti yaku Endori inayitana kuti wina abwere, ndi kukamutonhoza Sauli. Ndipo pamene mfiti inamuwona iye atayimirira, iye anati, “Ine ndikuwona mulungu akuwuka kuchokera padziko lapansi.”

⁹² Ndipo munthuyo atafa kale, kuyikidwa, ndi kuvunda mmanda, apa iye anali kuyima apo mu mphanga iyo, atavala mwinjiro wake wa mneneri; ndipo anali akadali mneneri, ameni, pakuti iye anati, “chifukwa chiani iwe unandiyitana ine kuchokera ku mpumulo wanga, powona kuti iwe wakhala mdani kwa Mulungu?” Muwoneni iye akulosea. “Mawa usiku, pa nthawi yino, iwe udzakhala ndi ine.” Iye anali akadali mneneri, ngakhale iye anali atachoka mu thupi ili.

Onani, iye anali atabwera apa ndipo anali gawo la Mawu amenewo, ndipo iye analowa kuchokera ku moyo wa thupi kubwerera mu thupi limene linali litakonzedwera kwa iye maziko adziko asanakhale. Iye analowa mu fiofane, chimene chinali Mawu. Inu mwamva izo? Ndiko kumene okhulupirira onse amapita pamene ife titembenuka kuchokera kuno.

⁹³ Ndiye, mmawonekedwe awo, chophimba ndiye chachotsedwa. Inu mukuona, inu ndinu Mawu, nanunso, pamene inu mulowa mmenemo. Ngati mwana wamng'ono; monga ine ndinanena kanthawi kapitako. . .

⁹⁴ Tsopano zindikirani. Yamikani Mulungu chifukwa chotsegula Zisindikizo izi, ndilo pemphero langa, kuti tidziwe zinthu izi!

⁹⁵ Tsopano vumbulutso loona la Melkizedeki likubwera powonekera. Chiani? Iye anali Mulungu, Mawu, Iye asanakhale thupi; Mulungu, Mawu. Chifukwa, Iye ankayenera kukhala; palibe wina aliyense akanakhoza kukhala wachisavundi monga Iye. Onani, ine ndinali nawo bambo ndi mayi; inu muli nawo, inunso. Yesu anali nawo bambo ndi mayi. “Koma Munthu uyu analibe bambo, kapena analibe mayi.” Yesu anali nayo nthawi imene Iye anayamba; Munthu uyu analibe. Yesu anapereka moyo Wake; Munthu uyu sakanakhoza, chifukwa Iye anali Moyo. Ndipo ali Munthu yemweyo nthawizonse. Ine ndikuyembekeza kuti Mulungu akuwulula izo kwa inu. Munthu yemweyo, nthawizonse.

⁹⁶ Zindikirani udindo Wake, “Mfumu ya chilungamo.” Tsopano, Ahebri 7:2, “Mfumu ya chilungamo, ndi Mfumu ya mtendere.” Iye ali mafumu awiri. Tsopano penyani, Ahebri 7:2, “Mfumu ya chilungamo, ndiponso Mfumu ya mtendere.” Iye ali mafumu awiri pamenepo. Tsopano pakuti Iye wabwera mu thupi nalandira thupi Lake mmwamba, mu Chivumbulutso 21:16, Iye akutchedwa, “Mfumu ya mafumu.” Iye ali atatu onse a iwo, palimodzi. Onani, Mfumu Mulungu, Mfumu Fiofane, Mfumu Yesu. “Iye ali Mfumu ya mafumu.”

Izo zonse zinakomana, monga ngati moyo, thupi, ndi mzimu, zonse zikubwera kudzapanga chimodzi.

⁹⁷ Ndiponso, Iye ali Atate, chimene chinali choyamba; Mwana; ndi Mzimu Woyera, Mzimu.

“Mfumu ya chilungamo,” chikhumbo cha Mzimu; fiofane, “Mfumu ya—ya mtendere,” fiofane; ndipo mu thupi Iye anali “Mfumu ya mafumu,” Munthu yemweyo.

⁹⁸ Pamene fiofane, Mose anamuwona Iye, Eksodo 33:2, Iye anali fiofane. Mose ankafuna kuwona Mulungu. Iye anali atamva liwu Lake, anamumva Iye akulankhula kwa iye, anamuwona Iye mu chitsamba pamenepo, ngati Lawi la Moto lalikulu. Ndipo iye anati, “Inu ndinu Yani? Ine ndikufuna kudziwa Yemwe Inu muli.” Mose anati. “Ine ndidzayika. . .” “Ngati Inu munirola ine kuti ndikuwoneni Inu, ine ndikufuna kuwona nkhope Yanu.”

⁹⁹ Iye anati, “Palibe munthu yemwe angakhoze kuwona nkhope Yanga.” Iye anati, “Ine ndidzayika dzanja Langa pamaso ako, ndipo ine ndidzadutsa pambali. Ndipo iwe ukhoza kuwona mbuyo Yanga, koma osati nkhope Yanga.” Mwaona? Ndipo pamene Iye anatero, inali mbuyo ya Munthu; anali fiofane. Ndiye

Mawu amene anabwera kwa Mose, “INE NDINE,” amenewo anali Mawu. Mawu anadza kwa Mose mwa mawonekedwe a Lawi la Moto mu chitsamba chonyeka, “INE NDINE.”

¹⁰⁰ Pamene Mawu ochokera ku zaumulungu . . . kuchokera ku fiofane, kani. Mundikhululukire ine. Iye anabwera kwa Abrahamu ngati Munthu, pansi pa mtengo wa thundu. Tsopano yang’anani apo. Apo panadza Munthu kwa Abrahamu, atatu a iwo, nakhala pansi pa mtengo wa thundu, atatu a iwo. Ndipo zindikirani, atatha Iye kulankhula kwa Abrahamu . . .

¹⁰¹ Nchifukwa chiani Iye anabwera? Abrahamu, pokhala mmodzi wokhala nalo lonjezo ndi uthenga wa mwana wakudza, ndiponso Iye anali mneneri wa Mawu a Mulungu amene anali kudalira Mawu a Mulungu, kutcha chirichonse chosiyana ngati kuti panalibe. Mukuona momwe Mawu aliri angwiro? Mawu anadza kwa mneneri. Onani, apo panali Mulungu mu fiofane. Ndipo Baibulo linati, “Mawu amadza kwa mneneri.” Ndipo apa panali m—Mawu mu fiofane.

Tsopano inu mukuti, “Kodi uyo anali Mulungu?”

¹⁰² Abrahamu anati uyo anali. Iye anati dzina Lake, linali, iye anamutcha Iye Elohim. Tsopano mu Genesis 1, inu mukupeza, “Pachiyambi *Elohim* analenga miyamba ndi dziko lapansi.” Mu Genesis 18, ife tikupeza kuti—kuti Abrahamu anamutcha Munthu uyu . . . amene anakhala pamenepo nalankhula kwa iye, ndipo amakhoza kumuuza iye zinsinsi za mtima wake, kumuuza iye zomwe Sarah anali kuganiza kumbuyo kwa Iye. Abrahamu anati, “Iye ndi Elohim.” Iye anali mmawonekedwe a fiofane. Inu mwamvetsa izo? Zindikirani zitatha . . .

¹⁰³ Tsopano ife tikupeza kuti Iye anali kenako mmawonekedwe a fiofane. Iye anamutcha Iye, “Ambuye Mulungu, Elohim.” Tsopano, mu Genesis 18, ife tikupeza kuti izo nzoona.

¹⁰⁴ Tsopano zindikirani Abrahamu. Analipo atatu a iwo palimodzi, koma pamene Abrahamu anakomana nawo atatu, iye anati, “Ambuye Wanga.”

Koma pamene Loti, kumusi mu Sodomu; awiri a iwo anatsikira uko, ndipo Loti atawawona awiri a iwo akubwera, ndipo iye anati, “Ambuye anga.” Mwaona, limene linali vuto? Malo oyamba, Loti sanali mneneri, uko nkulondola, kapena kuti iye anali mtumiki wa ora, kotero iye analibe vumbulutso lirilonse la Iye. Ndizo zolondola chimodzimodzi. Loti akanakhoza kuwatcha iwo “ambuye.” Dazeni la iwo, iye akanakhoza kunenabe kuti, “ambuye.”

Koma zinalibe kanthu kaya Abrahamu anawona angati, Iwo anali akadali Ambuye mmodzi. Apo pali Mulungu. Uyu anali Melkizedeki.

¹⁰⁵ Zindikirani, itatha kale nkhondo, Melkizedeki anamutumikira mwana Wake wogonjetsa mgonero; ganizani

za izo, gawo la Iyemwini! Tsopano ife tikufuna kuwona apa. Moyimira apa pali, mowonekera, mgonero. Itatha nkhondo, Iye anapereka za Iyemwini, chifukwa mgonero uli gawo la Khristu. Ndipo kulimbana kutatha, utatha iwe mwini kukwapulidwa, ndiye ndi pamene iwe umatenga gawo la Khristu, kukhala gawo la Umunthu uwu. Inu mwamvetsa izo?

¹⁰⁶ Yakobo anamenyera usiku wonse, ndipo sanamusiyeye Iye mpaka Iye atamudalitsa iye. Uko nkulondola. Kumenyera Moyo! Ndipo pakapita kuti nkhondo yatha, ndiye Mulungu amakupatsa iwe za Iyemwini. Uwo ndiwo mgonero Wake wona. Kabuledi kakang'ono ndi mkate basi kuyimira Iwo. Inu musamadye iwo kokha ngati inu mutamenyera iyo ndi kukhala gawo la Mulungu.

¹⁰⁷ Kumbukirani, pa nthawi iyi, mgonero unali usanayambitsidwe konse, osati mpaka isanachitike imfa ya Yesu Khristu, mazana ndi mazana ndi mazana a zaka kenako.

¹⁰⁸ Koma Melkizedeki, zitachitika kuti mwana Wake Abrahamu anapambana chigonjetso, Melkizedeki anakomana naye iye ndipo anamupatsa iye vinyo ndi mkate; kusonyeza kuti itachitika nkhondo yapadziko lapansi iyi yatha, ife tidzakomana naye Iye mmiyamba ndi kudya mgonero kachiwiri. Iwo udzakhala Mgonero wa Chikwati. “Ine sindidzamwanso za vinyo, kapena kudya chipatso, mpaka Ine nditadzadya icho ndi kumwa icho ndi inu, kwatsopano, mu Ufumu wa Atate Anga.” Nkulondola uko?

¹⁰⁹ Zindikirani kachiwiri, Melkizedeki anapita kukakomana naye Abrahamu iye asanabwerere kwawo. Ndi choyimira chokongola bwanji apa chimene ife tiri nacho! Melkizedeki kukomana naye Abrahamu iye asanabwerere kwawo, itatha nkhondo.

Ife tidzakomana naye Yesu mu mlengalenga, ife tisanafike Kwathu. Ndiko kulondola. Atesalonika Wachiwiri amatiuza ife izo, pakuti, “ife tidzakomana naye Iye mu mlengalenga.” Choyimira chokongola cha Rebekah kukomana naye Isaki, mmunda, mu kuzizira kwa tsiku. “Ife tidzakomana naye Iye mu mlengalenga.” Atesalonika Wachiwiri amatiuza ife choncho. “Pakuti ife amene tiri moyofe ndi kutsalira sitidzawaletsa kapena kuwasekereza iwo amene akugona; pakuti lipenga la Mulungu lidzawomba; akufa mwa Khristu adzawuka poyamba; ife amene tiri moyofe ndi kutsalira tidzakwatulidwa palimodzi nawo, kukakomana naye Ambuye mu mlengalenga.” Zangwiwo, zoyimira zonse izi.

¹¹⁰ Choncho, fiofane, ngati iwe wafa ndi kulowa mu fiofane iyo, (nchiani chimachitika?) fiofane imabwera ku dziko lapansi kudzalitenga thupi lowomboledwa. Ndipo ngati iwe uli mmwamba umu mumlengalenga, iwe udzalitenga thupi kukakomana nayo fiofane, ndi zimenezotu, “ndi

kukwatulidwira mmwamba, ndi kupita kukakomana naye Ambuye mu mlengalenga.”

¹¹¹ Melkizedeki uyu ndi ndani koma Mulungu!

¹¹² Tsopano ife tikuwona apa poyera chinsinsi chathunthu cha miyoyo yathu mu ulendo, ndipo imfa, ndi kumene ife tipita ife titafa. Ndiponso, kukonzedweratu kuli mwa kuwoneka kwa poyera apa. Tsopano mverani pamene ife tikuphunzitsa izi, mwatcheru.

¹¹³ Magawo a—a cholinga Chamuyaya chimene Iye anali nacho mu chinsinsi Chake tsopano chaululidwa. Zindikirani, akadalipobe magawo atatu ku ungwiro. Monga ngati Iye akuwombola dziko; njira yomweyo imene Iye akuwombolera Mpingo Wake. Iye akuwawombola anthu mu magawo atatu. Tsopano onani. Poyamba ndi kulungamitsidwa, monga Lutera analalikira; chachiwiri, kuyeretsedwa, monga Wesile analalikira; chachitatu, ubatizo wa Mzimu Woyera. Ndiko kulondola. Ndiye pakudza Mkwatulo!

¹¹⁴ Tsopano, dziko, kodi Iye anawombola chotani dziko? Choyamba, chimene Iye anachita, pamene ilo linachimwa, Iye analitsuka ilo mu ubatizo wa madzi. Ndiko kulondola. Ndiye Iye anakhetsera magazi Ake pa ilo, kuchokera pa mtanda, naliyeretsa ilo nalitcha ilo Lake Lomwe. Ndiyeno Iye akuchita chiyani? Pamene Iye anang’amba dziko lonse kulichotsa mwa inu, nachikonzanso chinthu chonse ndi ubatizo wamoto wa Mzimu Woyera, Iye adzalikonzanso dziko. Ndipo ilo lidzawotchedwa ndi Moto, ndi kuyeretsa nyongolosi iliyonse, kwa mailosi mamilioni utali wake, chirichonse chidzayeretsedwa. Ndiyeno pali Kumwamba Kwatsopano ndi Dziko lapansi Latsopano, monga ngati inu muli chorengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu pamene Mzimu Woyera ukugwirani inu. Onani, ndi zimenezotu, chinthu chonse chiri chabe chowonekera monga icho chingakhoze kukhalira. Chirichonse chiri mu utatu.

¹¹⁵ Kubadwa kwachirengedwe kuli patatu. Nchiani chinthu choyamba chimene chimachitika kwa mkazi yemwe akukhala ndi mwana? Nchiani chimatuluka poyamba? Madzi. Nchiani chimatuluka kachiwiri? Magazi. Kuchita kotsatira nchiani? Moyo. Madzi, magazi, mzimu.

Nchiani chimachitika kwa mbewu? Kuvunda. Chinthu choyamba nchiani? Phesi. Chotsatira nchiani? Ngayaye. Chotsatira nchiani? Mankhusu. Ndiye njere imatuluka kuchokera mwa iyo. Masiteji atatu chabe a iyo, mpaka iyo itafika ku njere. Ndizo chimodzimodzi.

¹¹⁶ Mulungu amatsimikizira izo. Izo nthawizonse zakhala zolondola. Mulungu amatsimikizira izo kukhala zoon. Kuwonetsa poyera, okonzedweratu ali amodzi okhawo amene akuganiziridwa mu chiwombolo. Kodi inu mwamva izo?

Ndiroleni ine ndinenenso izo. Okonzedweratu ali amodzi okhawo amene akuganiziridwa mu chiwombolo. Anthu akhoza kumapanga ngati, kumaganiza kuti iwo ali, koma chiwombolo chenicheni chiri iwo amene anakonzedweratu.” Chifukwa, mawu amene *kuwombola* amatanthauza “kubwezeretsa.” Nkulondola uko? *Kuwombola* ndi chinachake... *Kuwombola* chirichonse kuli, “kuchibwezeretsa icho ku malo ake apachiyambi.” Aleluya! Kotero ndi okonzedweratu okha amene ati adzabwezeretsedwe, chifukwa enawo sanabwere kuchokera Uko. Onani, “kubwezeretsa!”

¹¹⁷ Pokhala Amuyaya ndi Iye, pachiyambi... Moyo Wamuyaya umene inu munali nawo, lingaliro Lake la chimene inu munali, kokha, Iye ankafuna inu ku... Iye ankafuna kuti ine ndidzayime mu guwa, kunena. Iye ankafuna kuti inu mudzakhale pa mpando usikuuno. Ndiye ife tikutumikira cholinga Chake Chamuyaya. Ndipo mmodzi amene anachoka kwawo, anangobwera kokha ku dziko lapansi kudzatumikira cholinga Chake. Nkulondola uko? Chabwino. Ndiye, izo zitatha, izo zabweretsedwanso mu chikhalidwe cha ulemerero; izo zakhwima ndi kubweretsedwanso.

¹¹⁸ Nzosadabwitsa Paulo ankakhoza kunena, pamene iwo anali kupanga chipika kuti adulirepo mutu wake; iye anati, “O imfa, mbola yako ili kuti? O manda, chigonjetso chako chiri kuti? Koma kuthokoza kukhale kwa Mulungu Amene amatipatsa ife chigonjetso!” Iye anati, “Imfa, ndiuze ine kumene iwe ungakhoze kundipangitsa ine kufuula! Manda, ndiuze ine momwe iwe uti undigwirire ine! Pakuti, ine ndiri nawo Moyo Wamuyaya.” Ameni! Iye anzindikira izo. Imfa, gehena, manda, palibe chimene chingakhoze kumugwira iye. Ndipo palibe chimene chingakhoze kutipweteka ife, anali nawo Moyo Wamuyaya! Iye anzindikira kuti iye anadalitsidwa nawo Moyo Wamuyaya.

¹¹⁹ Monga ngati mame aang’ono. Ngati ine ndikumvetsa, ndiwo... Ine sindimadziwa zambiri za khemisitre. Koma, iko kuyenera kukhala kuti ndiko ku—kuwundana kwa nkhangungu kapena chikhalidwe. Ndipo pamene usiku ukhala wozizira ndi mdima, iwo amagwa kuchokera mmiyamba ndi kudonthera pa nthaka. Iwo amagwa kuchokera kwinakwake. Koma mmawa wotsatira dzuwa lisanatuluke, iwo akukhala pamenepo, mnyamata wamng’ono, akunjenjemera. Koma mungolola dzuwa lituluke, muliwone ilo likuyamba kunyezimira. Ilo ndi lokondwa. Chifukwa chiani? Dzuwa liyitanira iwo kubwerera kumene iwo anachokera.

Ndipo ndi momwe ziliri ndi Mkhristu. Aleluya! Ife tikudziwa pamene ife tiyenda kulowa mu Kukhalapo kwa Mulungu, chinachake mwa ife chimatiuza ife kuti ife timachokera kwinakwake, ndipo ife tikubwereranso mwa Mphamvu iyo imene ikutikoka ife.

¹²⁰ Mame apang’ono, iye amanyezimira ndi kuwala ndi kufuula, chifukwa iye akudziwa kuti iye anabwera kuchokera kumwamba uko, ndipo kuti dzuwa ilo lidzamutengeranso iye mmwamba.

Ndipo munthu yemwe ali chikhumbo cha Mulungu, wobadwa wa Mulungu, amadziwa, aleluya, pamene iye afika mu kukhudzana naye Mwana wa Mulungu, kuti iye adzakokeredwa mmwamba kuchokera kuno tsiku lina. “Pakuti ngati Ine ndikwezedwa mmwamba kuchokera pa dziko lapansi, Ine ndidzakokera anthu onse kwa Ine.” Ameni!

¹²¹ Tsopano zindikirani, tsopano, ife tikuwona Melkizedeki ndipo chifukwa chimene Maria sanali mayi Wake. Ndicho chifukwa Iye anamutcha iye “mkazi,” osati *amayi*. “Iye analibe bambo,” pakuti Iye anali Atate, Atate wosatha, atatu mwa Mmodzi. “Iye analibe mayi,” ndithudi ayi. Iye analibe atate, pakuti Iye anali Atate. Monga ndakatulo inanena nthawi yina, kukamba kuyamikira kwakukulu kwa Yesu, iye anati:

INE NDINE amene analankhula kwa Mose mu chitsamba chonyeka moto.

INE NDINE Mulungu wa Abrahamu, Nyenyezi Yowala ndi ya Mmawa.

INE NDINE Alfa, Omega, chiyambi kuchokera ku mathero.

INE NDINE chirengedwe chonse, ndipo Yesu ndilo Dzina. (Ndiko kulondola.)

O, inu mukuti Ine ndine Yani, ndipo iwo akuti Ine ndinachokera kuti,

Kodi inu mukuwadziwa Atate Anga, kapena kodi inu mungalidziwe Dzina Lawo? (Aleluya!)

¹²² Ndilo Dzina la Atate! Eya, “Ine ndinadza mu Dzina la Atate Anga, ndipo inu simunandilandire Ine ayi.” Mukuona? Zedi, Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.

¹²³ Ndipo Melkizedeki uyu anakhala thupi. Iye anadziwulula Iyemwini ngati Mwana wa munthu pamene Iye anadza, ngati Mneneri. Iye anadza mu maina atatu a Mwana; Mwana wa munthu, Mwana wa Mulungu, Mwana wa Davide.

¹²⁴ Pamene Iye anali pano padziko lapansi, Iye anali Munthu, kuti akwaniritse Lemba. Mose anati, “Ambuye Mulungu wanu adzawukitsa Mneneri wonga ine.” Kotero Iye anayenera kudza ngati Mneneri. Iye sanati, sananene konse, “Ine ndine Mwana wa Mulungu.” Iye anati, “Ine ndine Mwana wa munthu. Kodi inu mukumukhulupirira Mwana wa munthu?” Chifukwa, ndicho chimene Iye ankayenera kuchitira umboni, chifukwa ndicho chimene Iye anali.

Tsopano Iye wabwera mu Dzina lina la mwana, Mwana wa Mulungu; wosawoneka, Mzimu.

Ndipo pamene Iye adza kachiwiri, Iye ali Mwana wa Davide, kudzakhala pa mpandowachifumu Wake.

¹²⁵ Tsopano pamene Iye anali pano ndipo anapangidwa thupi, Iye ankatchedwa, “Mwana wa munthu.” Tsopano, Iye anadzipanga chotani Iyemwini kudziwika kwa dziko ngati Mwana wa munthu, Mneneri?

¹²⁶ Tsiku lina ine ndinawuzidwa nkhani ya Petro ndi Andrey, m’bale wake. Iwo anali asodzi, ndipo abambo awo a Yonasi anali wokhulupirira wakale wamkulu. Tsiku lina iwo anati iye anakhala pansu pambali pa ngalawa. Iye anati, “Ana, inu mukudziwa momwe ife tapempherera pamene ife timasowa nsomba.” Iwo anali asodzi ogulitsa nsomba. Iye anati, “Ife tadalira Mulungu, Yehova, kuti tikhale moyo. Ndipo ine ndikukulamba tsopano; ine sindingakhoze kukhala nanunso anyamata inu motalika. Ndipo ine nthawizonse, monga onse okhulupirira owona, ndayembekezera nthawi imene Mesiya uyo ati adzadze. Ife takhala nayo mitundu yonse ya abodza, koma pakudza Mmodzi weniweni, tsiku lina.” Ndipo iye anati, “Pamene Mesiya uyu adzadza, ine sindikufuna anyamata inu kuti mudzanyengedwe. Mesiya uyu sadzakhala wazamulungu chabe. Iye adzakhala Mneneri, pakuti mneneri wathu Mose, amene ife timutsatira, iye anati.”

Tsopano, Myuda aliyense adzakhulupirira mneneri wake. Iye amaphunzitsidwa kudziwa izo. Ndipo ngati mneneri anena chirichonse chimene chiri choncho, ndiye ndicho choonadi. Koma Mulungu anati, “Ngati pakhala mmodzi pakati panu, wauzimu, kapena mneneri, Ine Ambuye ndidzazipanga Ndekha kudziwika kwa iye. Ndipo ngati chimene iye anena chichitika, ndiye inu mumvereni iye ndi kumuwope iye; koma ngati izo sizitero, ndiye musamuwope iye konse.” Mwaona? Koteru uku kunali ku—kutsimikizira kwa mneneri.

¹²⁷ “Koteru Mose anali moona mneneri wotsimikiziridwa, ndipo iye anati, ‘Ambuye Mulungu wanu adzawukitsa, pakati panu, kuchokera kwa abale anu, Mneneri wonga ine. Ndipo onse amene sadzamvera iye adzadulidwa kuchokera kwa anthu.’” Iye anati, “Tsopano, ana, kumbukirani, kuti, monga Ahebri, ife timakhulupirira aneneri otsimikizidwa a Mulungu.” Tsopano mverani mwatcheru. Musati muphonye izo. Ndipo iye anati, “Pamene Mesiya adza, inu mudzamudziwa Iye, pakuti Iye adzakhala Mneneri-Mesiya. Tsopano, iwo anati izo zakhala zaka mazana anai. Ife sitinakhale naye kuchokera pa Malaki, koma iye adzakhala!”

¹²⁸ Tsiku lina, itachitika imfa yake, zaka pang’ono, mwana wake Andrey anali akuyenda motsatira gombe. Ndipo iye anamva munthu wa mthengo akuchokera mchikululu, akunena, “Mesiya uja akuyima pakati panu tsopano!” Mphungu yayikulu imene inakulira mchikululu ndi kuwulukira kumeneko, inati, “Mesiya

ali pakati panu pakali pano. Ife sitikumudziwabe Iye, koma Iye akuyima pakati panu. Ine ndidzamudziwa Iye, chifukwa ine ndidzawona chizindikiro chikubwera kuchokera Kumwamba.”

Tsiku lina iye anati, “Apo, taonani, pali Mwanawankhosa wa Mulungu amene achotsa tchimo la dziko!”

Kutali anapita...anapita munthu uyu, kuti akamupeze m'bale wake. Iye anati, “Simoni, ine ndikufuna iwe ubwere kuno; ife tamupeza kale Mesiya.”

“O, pitirira, Andrey! Iwe ukudziwa zabwino kuposa izo!”

“O, ine ndikudziwa. Koma, kuti, Munthu uyu ndi wosiyana.”

“Alikuti Iye? Kodi Iye amachokera kuti?”

“Yesu wa ku Nazareti.”

“Mzinda wawung'ono, woyipa uja? Bwanji, Iye sakanakhoza kubwera kuchokera ku malo oyipa, auve ngati awo.”

“Inu mungobwera ndi kudzawona.”

¹²⁹ Potsiriza anamunyengerera iye kuti abwere kumeneko tsiku lina. Kotero pamene iye anabwera patsogolo pa Mesiya uyu, Yesu atayima pamenepo, akulankhula kwa anthu. Pamene iye anayenda patsogolo pa Iye, Iye anati, “Dzina lako ndi Simoni, ndipo ndiwe mwana wa a Yonasi.” Izo zinachita icho. Iye anapeza mafungulo ku Ufumu. Chifukwa chiani? Iye anadziwa kuti Munthu uyo sanali kumudziwa iye. Ndipo kodi Iye anamudziwa bwanji iye, ndipo bambo wakale waumulungu uyo amene anali atamuphunzitsa iye momwe angakhulupirire Mesiya?

¹³⁰ Panali munthu atayima pamenepo, dzina lake Filipino. O, iye anatengeka kwenikweni! Iye anamudziwa munthu wina, anali akuperenga naye Baibulo. Kutali iye anapita, kuzungulira phiri, ndipo iye anamupeza iye kunja uko mu nkhalango yake ya azitona. Iye anali kugwada pansu, akupemphera. Iwo anali nawo maphunziro ambiri a Baibulo palimodzi, kotero iye anatuluka uko. Ndipo iye anati, iye atangotha kupyola mu kupemphera, iye anati, “Bwera, udzawone Amene ife tamupeza; Yesu wa ku Nazareti, mwana wa Yosefe. Iye ali Mesiya yemwe ife tikumuyembekezera.”

Tsopano ine ndikukhoza kumumva Nataniele akunena, “Tsopano, Filipino, iwe sunachoke pa mathero akuya, sichoncho iwe?”

¹³¹ “O, ayi. Iyai. Tsopano ndirole ine ndikuwuze iwe. Iwe ukudziwa, ife takhala tikuwerenga Baibulo palimodzi, ndipo kodi mneneri anati Mesiya adzakhala chiani?”

“Iye adzakhala Mneneri.”

“Iwe ukukumbukira nsodzi wakale uja kumene iwe unagulako nsomba, amene analibe maphunziro okwanira kuti alembe dzina lake, wotchedwa Simoni?”

“Eya. U-nhu.”

¹³² “Iye anabwera. Ndipo iwe ukudziwa chiani? Yesu uyu wa ku Nazareti anamuuza iye kuti dzina lake linali Simoni, anamusintha dzina lake kukhala Petro, limene liri “mwala wawung’ono,’ ndipo anamuuza iye amene anali abambo ake.”

“Chabwino,” iye anati—iye anati, “Ine sindikudziwa. Kodi chirichonse chabwino chingakhoze kubwera kuchokera ku Nazareti?”

¹³³ Iye anati, “Tiye tisalankhule za izo; ingobwera ndi kudzawona.” Ndilo ganizo labwilo, “Bwerani ndipo mudzawone.”

Kotero apa pakudza Filipino, akubwera naye Nataniele. Ndipo pamene iye anayamba kuyenda, Yesu mwina akuyima, akulankhula, mwina akupempherera odwala mu mzera wa pemphero. Ndipo pamene iye anadza kumene Yesu anali, Yesu anayang’ana pa iye, ndipo anati, “Taonani m’Israeli amene mwa iye mulibe choyipa.”

¹³⁴ Tsopano, inu mukuti, “Chabwino, munali momwe iye anavalira.” O, ayi. Onse akummawa amavala mofanana. Iye akanakhoza kukhala wa Chisiriya, kapena kukhala china chirichonse; ndevu, chovala.

¹³⁵ Iye anati, “Taonani m’Israeli mwa amene mwa iye mulibe choyipa,” mwa kulankhula kwina, “munthu woonamtima, wodzipereka.”

Chabwino, izo zinakhala ngati zinamuphwetsa Nataniele. Ndipo iye anati, “Rabbi,” chimene chimatanthawuza, “mphunzitsi.” “Rabbi, inu munandidziwa liti ine? Inu munadziwa bwanji kuti ine ndinali Myuda? Inu munadziwa bwanji kuti ine ndinali woonamtima, wopanda choyipa?”

¹³⁶ Iye anati, “Filipo asanakuyitane iwe, pamene iwe unali pansu pa mtengo, Ine ndinakuwona iwe.” Um! Mailosi khumi ndi asanu kutali, mbali yina ya dziko, tsiku ladzulo lake.

Kodi iye ananena chiani? “Rabbi, Inu ndinu Mwana wa Mulungu. Inu ndinu Mfumu ya Israeli!”

¹³⁷ Koma panayima ansembe awo apo, azawo-zawo, odzikhuthalitsa-okha, anati, “Munthu uyu ndi Bezezebule, wambwebwe.”

Yesu anati, “Ine ndikukhulukirani inu chifukwa cha izo.”

¹³⁸ Tsopano, kumbukirani, iwo sananene konse izo momveka, koma iwo ananena izo mu mitima yawo. “Ndipo Iye anazindikira malingaliro awo.” Uko nkulondola. Ndicho chimene Baibulo limanena. Itchani icho *misala* ngati inu mukufuna kutero, koma Iye—Iye anazindikira malingaliro awo.

¹³⁹ Ndipo Iye anati, “Ine ndikukhulukirani inu chifukwa cha izo. Koma tsiku lina Mzimu Woyera udzadza ndipo udzachita chinthu chomwechi ichi,” Iye kupita kale; “kulankhula

mawu motsutsa Iwo, simudzakhululukidwa mu dziko lino kapena dziko lakudza.” Nkulondola uko? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Tsopano, awo anali Ayuda.

Ndiye tsiku lina Iye anali nako kusowa kuti apite ku Samaria. Koma chabe ife tisanachite izo, ife tikumupeza mkazi, kapena . . .

¹⁴⁰ Mwamuna, pamene iye anapita kupyola mu chipata chotchedwa Chokongola, kuti iye anachiritsidwa. Ndipo Yesu anadziwa chikhalidwe chake, ndipo anamuwuzwa iye, “Yalula mphasa yako ndi kumapita kwanu.” Ndipo iye anachita izo, ndipo iye anakhala bwino.

Ndiye ife tikupeza kuti, Ayuda, ena a iwo anamulandira Iye. Ena anakhulupirira izo; ena sanakhulupirire. Nchifukwa chiani iwo sanakhulupirire izo? Iwo sanakonzedweretu ku Moyo. Iwo sanali gawo la chikhumbo chimenecho.

¹⁴¹ Tsopano kumbukirani, iwo anali ansembe ndi anthu aakulu. Ndipo Yesu . . . Ganizani za azamulungu awo ndi ansembe, anthu omwe inu simukanapeza chilema mmoyo wawo. Yesu anati, “Ndinu a atate anu mdierekezi, ndipo zintchito zake inu mukuchita.” Anati, “Ngati inu mukanakhala a Mulungu, inu mukanandikhulupirira Ine. Ngati inu simungakhoze kundikhulupirira Ine, khulupirirani—khulupirirani ntchito zimene Ine ndikuchita; izo zikuchitira umboni za Yemwe Ine ndiri.”

¹⁴² Tsopano, Baibulo linanena, kuti, “Yesu ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.” Yesu anati, “Ntchito zimene Ine ndichita adzachitanso iye amene akhulupirira pa Ine.” Uko nkulondola? Zindikirani, ameneyo anali Melkizedeki weniweni tsopano.

¹⁴³ Tsopano zindikirani, kachiwiri, panali mitundu itatu yokha ya anthu.

Inu mwandimvapo ine ndikunena kuti ine ndinali wa tsankho. Ine ndiri. Akhristu onse ndi a tsankho; osati tsankho la mtundu, koma tsankho la mzimu. Mtundu wa khungu la munthu ulibe chochita ndi iye. Iye ali mwana wa Mulungu mwa Kubadwa. Koma Mkhristu, Mulungu anati, “Ndipatulireni Ine!” “Tulukani kuchokera pakati pawo,” ndi zinazotero. Iye ali watsankho, wa zauve, pakati pa chabwino ndi cholakwika.

¹⁴⁴ Koma zindikirani, iwo anali nalo tsankho pamenepo, tsankho la mtundu, amene anali Asamaria.

Ndipo pali mitundu itatu yokha ya anthu pa dziko lapansi; ngati ife tikhulupirira Baibulo; ndiwo, anthu a Hamu, Shemu, ndi Yafeti. Ndiwo ana atatu a Nowa. Ife tonse tinachokera kumeneko. Uko nkulondola. Izo zimatipanga ife tonse kubwerera kwa Adamu, chimene chimatipanga ife tonse abale. Baibulo linati, “Mwa magari amodzi Mulungu analenga mafuko onse.” Ndife tonse abale, kupyolera mu mtsempha

wa magazi. Munthu wachikuda akhoza kumupatsa munthu woyera magazi, kapena mosinthanitsa. Munthu woyera akhoza kumupatsa—m’Japanizi, munthu wachikaso, kapena Mmwenye, munthu wofiira, kapena zina zonse, kapena wa Chiyafeti, kapena chirichonse, akhoza kumupatsa iye magazi, chifukwa ndife tonse amagazi ofanana. Mtundu wa khungu lathu, kumene ife timakhala, kunalibe chochita nazo izo.

Koma pamene ife tadzitsankha, ndi pamene ife timachoka mu dziko, monga Iye anatulutsira Israeli kuchokera mu Igupto. Ndipo pamene ife tadzisankha kuchokera ku zinthu za m’dziko.

¹⁴⁵ Tsopano, iwo anali anthu a Hamu, Shemu, ndi Yafeti. Ndipo ngati ife tikanakhala nayo nthawi kuti ife tiyendetse mibadwo mmbuyo, inu mukanakhoza kuwona Azungu, kumene iwo anachokera. Tsopano, ameneyo anali Myuda . . . Msamaria, amene anali theka Myuda ndi wa Mitundu, amene anakwatirana nawo Amitundu pa zochita za Balaamu, ndi Moabu. Iwo anali Asamaria. Ndipo uko kunali Ayuda ndi Amitundu.

Tsopano, ife Azungu tinalibe chochita nazo chirichonse cha izo. Ife sitinkakhulupirira Mesiya aliyense, ngakhale kanthu kalikonse. Ife sitinali kuyembekezera wina. Ife tinabweretsedwa mkati pambuyo pake.

Yesu anadza kwa Ake Omwe, ndipo Ake Omwe sanamulandire Iye. Ndipo Iye ananena kwa ophunzira Ake, “Musati mupite njira ya Amitundu, koma mupite kani kwa nkhusa zotayika za Israeli.” Ndipo Iye anapita kokha kwa nkhusa zotayika za Israeli. Ndipo penyani, Iye anadzikwaniritsa Iyemwini ngati Mwana wa munthu, pamaso pa Ayuda. Iwo anazikana Izo.

Tsopano, Asamaria, pokhala theka Myuda ndi Wamitundu, iwo ankakhulupiriranso, ndipo anali kuyembekezera Mesiya.

Ife sitinali. Ife tinali osapembedza, ndi ndodo pa nsana wathu, tikupembedza mafano; Amitundu.

¹⁴⁶ Koma tsopano tsiku lina, Yohane Woyera 4, Iye anali nako kusowa koti apite ku Samaria, pa njira Yake ya ku Yeriko. Koma anapita uko mozungulira Samaria. Ndipo pamene Iye anali kupita kumeneko, Iye anakhala pansu pa chitsime kunjja kwa mzinda wotchedwa Sukari. Ndipo chitsime, ngati inu munayamba mwafikako uko, ndi amawonekedwe abwino aang’ono pafupi onga awa pano. Ndipo kuli kasupe wa aliyense kumeneko, wa madzi, pamene iwo onse amabwera. Ndipo akazi amabwera mmawa, kudzatunga mitsuko yawo ya madzi, ndi kuyiyika iyo pa mitu yawo, ndipo umodzi pa phewa lirilonse, ndipo ndikuyenda nayo iyo basi molunjika monga angathere, osadonthetsa dontho; kulankhulana wina ndi mzake. Koteru, iwo amakhoza, anthu amakhoza kubwera kunjja uko.

147 Kotero iyi inali pafupi 11:00 koloko masana. Kotero Iye anawatuma ophunzira Ake mu mzinda, kuti, akagule zitumbuwa zina, chakudya. Ndipo pamene iwo anali atapita . . .

148 Panali mkazi yemwe anali wa mbiri-yoyipa. Ife tikanamutcha iye, lero, mkazi wa getsi lofiira, kapena kahule. Iye anali nawo amuna ambiri. Kotero pamene Yesu anali atakhala apo, mkazi uyu anatulukira ili pafupi 11:00 koloko. Onani, iye sakanakhoza kubwera nawo anamwali pamene iwo amabwera mmawa kuti adzatunge madzi awo ochapira; iye anachita kuyembekezera mpaka iwo onse . . . Iwo sankasakanizana monga iwo amachitira tsopano. Iye ankadziwika. Koterono, iye anatulukira kudzatunga madzi ena, kotero iye anangotenga chotungira chakale, ndi kuyika zingwe ku chotungira, nayamba kuchitsitsa icho.

Iye anamva Wina akunena, “Mkazi, ndibweretsere Ine akumwa.” Tsopano, kumbikirani, uyu ndi Melkizedeki. Uyu ndi Yesu, dzulo, Mwana wa munthu.

149 Ndipo iye anayang’ana pozungulira, ndipo iye anawona Myuda. Kotero iye anati, “Bwana, sichabwino kuti Myuda amufunse Msamaria chirichonse. Ine ndine mkazi wa ku Samaria, kotero Inu mwalankhula kudzichotsa pa malo Anu. Inu simmayenera kundipempha ine chinthu chonga icho. Ife tiribe chochita wina ndi mzake.”

150 Iye anati, “Koma ngati iwe ukanadziwa Amene amalankhula nawe iwe, iwe ukanandipempha Ine akumwa.”

Iye anati, “Inu mutunga chonani iwo? Chitsimechi nchakuya, ndipo Inu mulibe chotungira.”

151 Iye anati, “Madzi amene Ine ndimapereka ndi Madzi a Moyo, otumphukira ku Moyo Wamuyaya.”

Iye analankhula naye iye mpaka Iye anapeza chimene chikhaliidwe chake chinali. Ndiyeno ndi . . . Penyani chimene Iye ananena kwa iye tsopano, “Pita ukatenge mwamuna wako ndipo ubwere kuno.”

Ndipo iye anati, “Ine ndiribe mwamuna.”

152 Iye anati, “Iwe wanena zoono, pakuti iwe wakhala nawo asanu, ndipo mmodzi amene iwe uli naye tsopano sali wako ayi. Kotero, mu ichi, iwe wanena zoono.”

Onani kusiyana kwa pakati pa mkazi uyo ndi gulu lija la ansembe. Iye ankadziwa zochuluka za Mulungu kuposa momwe gulu lonse ilo la ansembe linkadziwira, atayikidwa pamodzi.

153 Iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Inu ndinu Mneneri.” Iye anati, “Ife sitinakhale naye wina kwa zaka mazana anayi. Tsopano, ife tikudziwa kuti Mesiya akubwera. Ndipo pamene Mesiya adza, ndicho chimene Iye ati adzachite.” Icho chinali chizindikiro cha Mesiya, pakuti Iye anali Mwana wa munthu.

Anati, “Ndicho chimene Iye ati adzachite pamene Iye adza. Inu muyenera kukhala mneneri Wake.”

¹⁵⁴ Iye anati, “Ine ndine Iye.” Palibe aliyense angakhoze kunena izo.

¹⁵⁵ Iye anagwetsa mtsuko wa madzi uwo nathamangira mu mzinda, ndipo anati, “Bwerani, mudzawone Munthu Amene wandiuzza ine zimene ine ndachita. Kodi sali uyu Mesiya amene?”

Tsopano kumbukirani, Iye analonjeza kudzachita chinthu chomwecho pa mapeto a mtundu wa Amitundu.

Ayuda anali nazo zaka zikwi zinai kuti amuyang’anire Mesiya uyo, zaka zikwi zinai za kuphunzitsa kuti Iye anali kudza, ndi zimene Iye ati adzachite pamene Iye adzafike uko, ndipo iwo analephera kumuwona Iye, kapena kulephera kuzindikira izo. Ndipo pamene Iye anadzidziwitsa Yekha mu kanenedwe kamene ka Baibulo komwe Iye anati Iye adzachita, pamene Iye anali atakhala mu fiofane ndiyeno nkukhala thupi nakhala pakati pawo, iwo analephera kuwona izo, ndipo anatcha ntchito Zake ntchito za mdierekezi.

¹⁵⁶ Tsopano ife takhala nazo zaka zikwi ziwiri za kuphunzitsa, kutsika kupyolera mu mpingo wa Aroma Katolika, atapita atumwi. Ndiye ife tinabwera mmusi kupyola mu Roma Katolika, Agriki, ndi zina zotero, mpaka mmusi ku m’badwo wa Lutera, ndi Wesile, zinazonse, mabungwe mazana asanu ndi anayi kubwera pansu. Iwo anali nako kuphunzitsa kwa mibadwo yonse.

Tsopano Iye analonjeza, chabe nthawi yotsiriza isanafike, kuti chithunzi cha Sodomu ndi Gomora chidzabweranso, “Monga zinaliri mmasiku a Sodomu, chotero izo zidzakhala mu kudza kwa nthawi yotsiriza, Mwana wa munthu adzadzizwulula Yekha kachiwiri.” [Malo osajambulidwa patepi—Mkonzi.]

“Komabe kanthawi pang’ono ndipo dziko silidzandiwonanso ine; komabe inu mudzandiwona Ine, pakuti Ine,” pulonauni wa iyemwini, “Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka ku matsiriziro, mathero a dziko. Ine ndidzakhala ndi inu.” Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse. Inu mukuona?

¹⁵⁷ Inu mukuona, *Msamaria* anali, makamaka, kuchokera mu ulaliki wanga wa usiku watha, anali Hagara, onani, choyimira chopotozedwa. *Myuda* anali Sarah, kapena anali M’sarai. Koma wa *Amitundu* ndi wa Maria, Mbewu Yachifumu, Mbewu Yachifumu ya Abrahamu.

¹⁵⁸ Tsopano ndi zolonjezedwa kuti mmasiku otsiriza awa, kuti, Mulungu yemweyu, Khristu yemweyu, akanabwereranso kuno nadziwulula Iyemwini ngati Mwana wa munthu.

Chifukwa chiani? Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse. Ndipo ngati Iye anawalola Ayuda awo kupita nazo,

nawapatsa iwo chizindikiro cha Mesiya icho, ndiyeno kubwera kumathero a kuphunzitsa kwa Amitundu ndi kungowalola iwo kupita mu zamulungu, Iye adzakhala wopanda chilungamo. Iye ayenera kuchita chinthu chomwecho, chifukwa Baibulo linati mu Sati- . . . Ahebri 13:8, “Iye ali yemweyo.”

Ndipo Iye walonjeza mu Malaki 4, ndi Malemba onse osiyana, kuti, masiku otsiriza, mpingo udzakhala ukukhala chimodzimidzi basi monga izo ziliri lero, ndipo dziko lidzakhala.

¹⁵⁹ Yang’anani pa dziko lero. Yang’anani pa chikhalidwe cha Sodomu. Yang’anani pa zivomezi mu malo osiyana, ndi zinthu zimene zikuchitika. Yang’anani pa mpingo ndi chisokonezo chimene iwo ulimo, cha Babeloni. Yang’anani pa mtumiki kwa iwo, Oral Roberts ndi Billy Graham.

G-r-a-h-a-m, nthawi yoyamba imene ife tinakhalapo naye mtumiki, ku mipingo yonse, imene dzina lake linatherapo mu h-a-m, ngati Abraham. A-b-r-a-h-a-m ndi zilembo zisanu ndi ziwiri. G-r-a-h-a-m ndi zilembo zisanu ndi chimodzi. Kodi ali kuti iye? Kudziko. Sikisi ndi chiwerengero cha munthu. Munthu analengedwa pa tsiku lachisanu ndi chimodzi. Koma seveni ili chiwerengero cha Mulungu.

¹⁶⁰ Tsopano yang’anani pa iwo kumusi uko mu Sodomu. Ndipo apo pali atumiki awo kumusi uko akulankhula kwa iwo.

Komano ilikuti Mbewu yachifumu ya Abrahamu’yo? Chizindikiro chawo chiri kuti, chimene Iye anati? “Monga izo zinaliri mu masiku a Sodomu,” mmene Mulungu anabwera pansu ndipo anawonetseredwa mu thupi la munthu, ndipo anamuwuzza zimene Sarah anali kuganiza kuseri mu mtima wake, mu chihema kuseri kwa Iye, chizindikiro chotsiriza dziko la Amitundu lisanawonongedwe ndi moto. Ndipo Mpingo uli nacho chizindikiro chake chotsiriza dziko lonse lisanawonongedwe, ufumu wa Amitundu uwu udzawonongedwa ndi moto ndi mkwiyo wa Mulungu. Kodi inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.]

¹⁶¹ Melkizedeki uyo anali thupi, kudziyimira Iyemwini mu thupi la munthu; ndiyeno kenako Iye anapangidwa thupi. Ndipo tsopano, usikuuno, Iye ali yemweyo, dzulo, lero, ndi nthawizonse. Kodi inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.]

¹⁶² Melkizedeki uyu ndi ndani, ndiye, ndiye yemweyo dzulo, lero. . . “Analibe konse bambo, analibe konse mayi; Iye analibe konse chiyambi cha masiku, Iye analibe konse mathero aliwonse a moyo.” Ndipo Iye anakomana naye Abrahamu, ndipo kodi Iye anachita chizindikiro cha mtundu wanji? Ndiye pamene Iye anapangidwa thupi, Iye anati izo zidzabwerezanso kumene nthawi yotsiriza isanakwane. Kodi inu mukukhulupirira izo?

[Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Ine ndikukhulupirira izo. [“Ameni.”]

Tiyeni tipemphere.

¹⁶³ Wokondedwa Mulungu, ine ndikukhulupirira Malemba, kuti Inu mwanena kuti Inu munalu “yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.” Ndipo moonamtima mu mtima mwanga, Ambuye, ine ndikudziwa kuti chinachake chikukonzekera kuchitika. Ine sindingakhoze kuzindikira izo motsimikiza. Ine ndikuwopa kuti ndinene chirichonse, Ambuye. Inu mukudziwa mtima wa wantchito Wanu.

¹⁶⁴ Ndipo ndi nthawi zingati, kupyola mu m’badwo pamene Inu munkatumiza zinthu, anthu nalephera kumvetsa izo. Munthu mosasintha akupembedza Mulungu pa zomwe Iye anachita, ndi kunena zinthu zazikulu zimene Iye ati adzachite, koma kusalabadira zimene Iye akuchita. Chomwecho zakhalapo kupyola mu m’badwo. Nchifukwa chiani mpingo wa Roma umalephera kuwona Patreki Woyera ngati mneneri wa Mulungu? Nchifukwa chiani iwo anapha Joan wa ku Arc pamene iye anali—mneneri wamkazi, kumutentha iye ngati mfiti? Atate, nthawizonse nzakale. Inu mumazibisa izo ku maso a anzeru ndi aluntha. Nzosadabwitsa Inu munanena kwa iwo ansembe, “Inu mumakongoletsa manda a aneneri, ndipo ndinu amene munawayika iwo mmenemo.” Iwo atapita kale, iwo amawona kulakwitsa kwawo. Iwo nthawizonse amakunzuzani Inu, Ambuye, mmawonekedwe aliwonse amene Inu munabwereramo.

¹⁶⁵ Ine ndikupemphera, usiku uno, Mulungu, nthawi imodzi yina yokha. Mawa ife takonza kudzakhala...tikupita ku Tucson. Mbali zina za dziko, mizinda yina ife tiyenera kulalikiramo. Koma, Wokondedwa Mulungu, pakhoza kukhala alendo pano usikuuno amene sanati nkomwe... Iwo amvapo Mawu akulalikidwa, koma sanawawonepo Iwo akuwonetseredwa.

Monga ine ndinakupemphani Inu pachiyambi. Pamene ophunzira awo, Kleopa ndi mnzake, akubwera kuchokera ku Emausi, anali kuyenda motsatira njira, ndipo Inu munalumphira kuchokera mu tchire ndi kuyamba kulankhula nawo iwo, chitachitika chiwukitsiro, munalalikirira kwa iwo. Bwanji, Iye anati, “Opusa, ofooka mtima. Kodi inu simukudziwa kuti Khristu ayenera kuvutika zinthu izi, ndi kulowa mu ulemerero Wake?” Komabe iwo sanazindikire izo. Utali wa tsiku lonse iwo anayenda nanu Inu, ndipo sanakudziwenibe Inu. Koma usiku wina...

Usiku utadza, iwo anakuwumirizani Inu kuti mulowe mnyumba. Pamene iwo analowa mu nyumba ya alendo yaying’ono natseka zitseko, ndiye Inu munachita chinachake chabe momwe Inu munachitira izo chisanachitike chipachikiko

Chanu, ndipo iwo anazindikira kuti anali Khristu wowukitsidwa. Mu mphindi pang'ono Inu munali kuseri kwa makatani ndipo mutapita. Mwamsanga iwo anathamanga nawauza ophunzira, “Ambuye awuka indedi!”

¹⁶⁶ Atate, Mulungu, ine ndikukhulupirira kuti Inu mukadali amoyo. Ine ndikudziwa kuti Inu muli. Ndipo Inu mwatsimikizira izo kwa ife nthawi zambiri. Kodi Inu mungakhoze kungochita izo kamodzinso kwa ife, Ambuye? Ngati ife titi tipeze chisomo pamaso Panu, lolani kuti izo zichitike kamodzinso. Ine ndine wantchito Wanu; awa ndi antchito Anu muno. Ambuye, zonse zimene ine ndanena sizingawundane ku. . . Mawu amodzi chabe ochokera kwa Inu adzakhala oposa amene ine ndanena mu usiku usanu uwu, kapena mauthenga asanu. Zidzakhala zochuluka, mawu amodzi chabe ochokera kwa Inu. Kodi Inu simulankhula, Ambuye, kuti anthu akhoze kudziwa kuti ine ndawawuza iwo Choonadi? Perekani izo, Mulungu. Ine ndikupempha izi mu Dzina la Yesu, izi kamodzi akanso. Amenii.

¹⁶⁷ Tsopano, ine sindikukudziwani inu. Ine ndikudziwa anthu ena. Ine ndikumudziwa mnyamata uyu amene wakhala *apa*. Ine ndikumudziwa Bill Dauch wakhala pomwe *apo*. Ine ndikufuna ku. . . Apa pali M'bale Blair, Rodney Cox. Ndi kovuta kuwona kunjako.

Pa mbali *iyi*, pa nthawi ino kumene ine sindingakhoze kupenya aliyense, kwenikweni, yemwe ine ndikumudziwa.

¹⁶⁸ Tsopano ndi angati muno amene akudziwa kuti ine ndine mlendo kwa inu? Kwezerani mmwamba manja anu, amene akudziwa kuti ine sindikudziwa kanthu za inu, kwezani manja anu mbali zonse.

Ndi angati mkati muno amene ali nacho chinachake chovuta, kapena chinachake chimene inu mukudziwa kuti ine sindikudziwa kanthu kake? Mungakwezere mmwamba manja anu.

Tsopano, izo zingakhale kwathunthu, mtheradi kwathunthu zosatheka kuti ine ndidziwe chirichonse za inu. Ngati ndi choncho, ndiye, ziyenera kubwera kuchokera ku vumbulutso lina la Mzimu.

Ndipo pokhala kuti ine ndakuuzani inu mausiku onse awa, ndi usikuuno, kuti Iye sali wakufa; Iye ali pano, ndipo analonjeza kudzachita chinthu chomwecho. Ndipo analonjeza kuti padzafika nthawi mmasiku otsiriza, molingana ndi Malaki 4 ndi molingana ndi Luka Woyera, imene Iye ati adzawonekerenso mmawonekedwe a munthu pakati pa anthu Ake nachita zinthu zomwezo, naulula chinthu chomwecho, chizindikiro chomwecho cha Umesiya. Ndi angati akudziwa izo, inu owerenga Baibulo, mumadziwa kuti ndicho Choonadi? Nenani, “Amenii.” [Osonkhana anena, “Amenii.”—Mkonzi.] Muyenera kukhala nonse owerenga Baibulo.

169 Tsopano, ine ndikudziwa kuti nzachirendo kwa anthu lero, komabe ndicho Choonadi. Ndicho chifukwa iwo sanamudziwe Yesu wa ku Nazareti. Iwo ankadziwa zikhulupiriro za mpingo wawo, koma iwo sankamudziwa Iye. Koma Iye anadza chabe momwe Baibulo linanenera; osati azamungu, osati wansembe. Iye anadza ngati Mneneri, ndipo Ake Omwe sanamulandire Iye.

170 Tsopano, ngati Mulungu ati asunge Mawu Ake, ndipo ngati ine ndipezeka kuti . . . zichitika kuti zikagwere pa wina amene ine ndikumudziwa, ndiye ine ndidza—ine ndidzapeza winawake. Onani, ine ndikufuna wina amene ine sindikumudziwa. Ndipo ine ndikufuna kuti inu mupemphere.

171 Tsopano, onani, panali mkazi wamng’ono wina nthawi yina amene anali ndi sautso. Iye anali atawononga ndalama kwa madotolo; iwo samakhoza kumuchitira iye chabwino. Ndipo iye ananena mu mtima mwake, “Ngati ine ndingakhoze kukhudza zovala za Mwamuna uja, ine ndidzakhala bwino.” Inu mukuyikumbukira nkhanayo? Ndipo kotero onse a iwo anayesa kumupangitsa iye kuti akhale kumbuyo, koma iye anazipanikiza kupyola mpaka iye anakhudza chovala Chake, anabwerera nakakhala pansa.

172 Tsopano mverani mwatcheru. Ndiyeno pamene Iye anachita izo, pamene iye anachita izo, Yesu anatembenuka ndipo anati, “Ndani wandikhudza Ine?”

173 Bwanji, Petro mtumwi anamutsutsa Iye. Mwina Iye ananena chinachake chonga, “Ambuye, musanene chinthu chotero. Anthu adzakhulupirira kuti pali chinachake cholakwika ndi Inu. Chifukwa, pamene Inu munawafunsa iwo kuti adye thupi Lanu ndi kumwa Magazi Anu, iwo anaganiza kale kuti pali china cholakwika. Ndipo Inu mukuti, ‘Ndani wandikhudza Ine?’ Bwanji, unyinjira wonse u-kukukhudzani Inu.”

174 Iye anati, “Inde, koma Ine ndikuwona kuti ukoma wachoka mwa Ine.” Uko kunali kukhudza kwa mtundu wina. Tsopano, aliyense akudziwa kuti *ukoma* ndi “mphamvu.” “Ine ndafooka; ukoma nandichokera Ine.”

Ndipo Iye anayang’ana pozungulira pa omvetsera mpaka Iye atamupeza mkazi wamng’ono, namuza iye za vuto lake la kutaya magazi. Ndipo iye anamverera mu thupi lake kuti vuto lotaya magazi lija linali litayima. Nkulondola uko? Ndipo Iye anati, “Chikhulupiriro chako chakupulumutsa iwe.”

Tsopano, mawu Achigriki ake ndi *sozo*, amene amatanthawuza mwamtheradi “kupulumutsidwa,” mwathupi kapena mwauzimu, zofanana basi. Iye “anapulumutsa.” Iye ali—Iye ali Mpulumutsi wanu.

175 Tsopano, ngati izo zinali Iye dzulo, ndipo momwe Iye anachitira, kutsimikizira kuti Iye anali pakati pa anthu, Mesiya analonjeza; ndipo ndimo momwe Iye anazizindikiritsira Iyemwini, nalonjeza mwa Baibulo, Iye adzachita chinthu

chomwecho tsopano; sangatero Iye, kodi Iye sangachite chinthu chomwecho?

¹⁷⁶ Inu mukuti, “Kodi Iye ananena za kuchiritsa odwala?” Eya!

Ahebri, Baibulo limene ine ndangowerengako kumene, ananena kuti, “Yesu Khristu tsopano ali Wansembe Wamkulu wathu amene akhodza kukhudzidwa ndi kumverera kwa zopweteka zathu.” Ndi angati amadziwa kuti izo nzoona? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Baibulo linanena izo. “Iye ali Wansembe Wamkulu tsopano amene akhoza kukhudzidwa ndi zomverera za zopweteka zathu.” Ndiye ngati Iye ali Wansembe Wamkulu yemweyo amene Iye anali pamenepo, Iye angachite motani tsopano? Iye adzayenera kuchita mwanjira yomweyo imene Iye anachitira pamenepo, ngati Iye ali Wansembe Wamkulu yemweyo. Tsopano, inu mukhoza . . .

Ine sindine Wansembe Wamkulu wanu. Inu mukhoza kundikhudza ine, ndipo izo zikhoza kukhala monga ngati kuwakhudza amuna anu, kapena m’bale wanu, kapena chinanso, munthu.

¹⁷⁷ Koma inu mulole chikhulupiriro chanu chimukhudze Iye, ndipo muwone chimene chiti chichitike. Tsopano, ngati ine ndiri wantchito wa Mulungu ndipo ndakuuzani inu Choonadi, Mulungu adzatsimikizira izo kukhala Choonadi. Ndipo izo zidzatsimikizira kuti Yesu Khristu ali moyo usiku uno, akuyima pano. Nkulondola uko? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.]

Tsopano, inu muli nacho chikhulupiriro, mbali imodzi chabe pa nthawi, mbali imodzi. Inu muli nacho chikhulupiriro kunjira uko. Ine kulibwino ndikhale pa cholankhulira apa, chifukwa iwo sangakhoze kundimva ine.

¹⁷⁸ Winawake atangoyang’ana mmwamba kwa Mulungu, ndi kunena, “Mulungu, munthu uyo sakundidziwa ine. Iye sakudziwa kanthu za ine. Ndine mlendo mwangwiwo kwa iye. Koma mulole chikhulupiriro changa chikukhudzeni Inu, Ambuye. Ndipo Inu mukudziwa limene liri vuto ndi ine, Ambuye. Inu mukudziwa zonse za ine. Inu mukudziwa yemwe ine ndiri, momwemo monga Inu munadziwira yemwe Petro anali, mofanana monga Inu munamudziwira Nataniele, monga Inu munadziwira chimene chinali cholakwika ndi mkazi wa kuwukha magazi. Ndipo munthu uyu akundiuzwa ine kuti Ndinu ‘yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse.’ Ndiye, Ambuye, mulole chikhulupiriro changa kuti chikukhudzeni Inu.”

Ndipo ngati Iye atachite izo, ndipo mosalephera nazitsimikizira Iyemwini pano, ndi angati a inu ati amukhulupirire Iye ndi mtima wanu wonse; ngati Iye ati achite izi mmodzi yekha, kapena awiri, kapena anthu atatu, kwa—kwa umboni? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Mulungu adalitse inu.

¹⁷⁹ Tsopano, Atate Mulungu, izi ziri kwathunthu kunja kwa manja a munthu aliyense. Izo zidzayenera kukhala chopambana chazimu. Kotero ine ndikupemphera kuti Inu mudzandithandize ine tsopano, Ambuye. Ine ndiri mmanja Mwanu. Chitani nane ine pamene Inu mukuona koyenera. Mu Dzina la Yesu. Amen.

¹⁸⁰ Tsopano, musati mukhale amanjenje. Modzichepetsa basi, mwaulemu nenani, “Ambuye, ine ndidzakutumikirani Inu. Ndipo izo zidzakhala zoono, kuti, ngati ine ndingakhoze kukhudza chovala Chanu, ndiye Inu mulankhulenso kupyolera mwa munthu uyo. Izo zidzatsimikizira kwa ine kuti zimene iye wanena ziri Choonadi.” Nkulondola uko?

¹⁸¹ Ndi angati anawonapo chithunzi cha Kuwala kuja? Ichochi konsekonse pa dziko, kulikonse. Sayansi yajambula iko ndi kukuyesa iko, ndipo kulikonse. Tsopano, Iye ali pomwe pano tsopano; Mmodzi yemweyo amene ananena za *Chikwati Ndi Chilekano*, Mmodzi yemweyo amene anali pa phiri, anagwedeza mapiri kumbuyo uko, Mmodzi yemweyo wa kumusi uko ku mtsinje mu ‘33, yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse. Iye ali yemweyo. [M’bale Branham ayimikira—Mkonzi.]

¹⁸² Tsopano, pali mkazi, ndipo iye akuzindikira tsopano kuti chinachake chachitika. Kuwala kuja kukupachikika pa iye pomwe. Iye wakhala pomwe *apa*, wavala juzi ya girini, kapena chinachake. Ine sindikumudziwa mkaziyo. Ine ndikuganiza kuti ndife alendo kwa wina ndi mzake. Izo nzolondola. Kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu... Inu muli—inu mu kusowa chichachake, ndipo kodi inu mukukhulupirira kuti Mulungu akhoza kuwulula kwa ine limene liri vuto lanu? Ndipo ngati Iye atero, ndiye inu mukudziwa kuti idzayenera kukhala mphoto yauzimu, chifukwa ine sindikukudziwani inu. Ndipo izo zidzayenera kubwera kupyolera mu chazimu.

Zitengera pa zomwe inu mukuganiza kuti izo ziri. Inu mukhoza kutenga mbali yanu ndi ansembe, kuchitcha icho “mdierekezi,” kapena mukhoza kutenga mbali ndi wokhulupirira ndi kuchitcha icho “Mulungu.” Chirichonse chimene inu mukhulupirira, ndiko kumene mphoto yanu idzachokereko.

¹⁸³ Ngati Mulungu ati awulule kwa ine vuto lanu, kodi inu mumulandira Iye ngati chanu—chitetzero chanu cha vuto ilo? Ine sindikudziwa lomwe vutolo liri. Koma ine ndikudziwa, ndipo inu mukudziwa, kuti chinachake chikuchitika.

¹⁸⁴ Tsopano, tsopano mungondirola ine ndikuuzeni inu momwe inu mukumverera, ndiyeno inu mudzadzziwa; kumverera kofundira, kokoma, kwawofuwofu. Ine ndikuyang’ana molunjika kumene pa Iko. Ndiko Kuwala uko, Kuwala kwa ambara kumene kwapachikika pa mkaziyo.

Ndipo donayo akuvutika ndi vuto mu mimba yake. Ndicho chokhala ngati chophuka, monga, mu mimba yake. Iye si wochokera kuno. [Mlongo anena, “Kulondola.”] Ayi. Ndinu ochokera kutali ndi kuno sichoncho inu? Uko nkulondola. Ndinu wochokera ku Wisconsin. Nkulondola uko? Zedi. Tsopano inu mwachiritsidwa. Chikhulupiriro chanu chakupangani inu wamphumphu.

¹⁸⁵ Tsopano tandiuzani ine Amene wamukhudza mkaziyo? Ine ndiri mayadi makumi awiri ndi asanu kuchokera kwa iye. Iye anakhudza Yesu Khristu, Wansembe Wamkulu. Kodi inu mukukhulupirira izo? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.]

¹⁸⁶ Ine ndikuyang’ana pa mkazi amene ine ndinalankhula naye. Mkazi uyu, ine ndikuyang’ana kumene pa iye, chifukwa iye akupempherera zolimba kwambiri mwamuna. Iye anandiuza ine kuti iye anali ndi mwamuna . . . Iye sanandiuze ine kanthu za izo.

Kodi dzina lake liri Akazi a Waldrop. Iye amachokera ku Phoenix. Iye anawukitsidwa kwa akufa, ndipo adotolo ake anabwera ndi chojambulira nawonetsa khansala mu mtima mwake. Iye anafera mu mzera wa pemphero. Kodi izo zakhala motalika bwanji, Akazi a Waldrop? Zaka khumi ndi zisanu ndi zitatu zapitazo, ndipo apo iye wakhala usikuuno, umboni mamoyo. Adotolo ake abwera ku msonkhano, abweretsa . . . Anati, “Mkaziyo angakhale moyo chotani?” Koma ndi uyo apo, ndipo wopanda chizindikiro cha iyo.

¹⁸⁷ Iye wabweretsa winawake, ndipo iye akumupempherera iye. Tsopano, iye akufa, ndi matenda a shuga. Tsopano, izo ine ndimadziwa. Koma pokhala kuti inu mukupemphera . . . Inu mukudziwa kuti ine sindikudziwa yemwe iye ali, Akazi a Waldrop.

¹⁸⁸ Iye ali wochokera ku Missouri, ndipo dzina lake ndi Bambo Cooper. Uko nkulondola. Tsopano, inu mukukhulupirira, inu mukhoza kubwerera kwanu ndi kukakhala bwino, bwana. Izo ziri kwa inu, ngati ine muti mukhulupirire izo.

¹⁸⁹ Apa pali mkazi, ndipo iye akuvutika ndi chikhalidwe cha mphumu, zosokonezeka. Iye sakuchojera kuno. Iye wakhala mu khamu ilo, kunja *uko*. Ine ndikuyembekeza kuti iye akumva . . . Iye sakuchojera kuno. Iye akuchokera ku Georgia. Abiti McKenny. Kodi inu mukukhulupirira ndi mtima wanu wonse, ndipo mukukhulupirira kuti Mulungu akupangani inu wabwino? Imani pa mapazi anu, ngati ndinu mlendo kwa ine ndipo izo nzoona. Yesu Khristu wakuchizani inu. Kodi inu mukukhulupirira?

[M’bale Branham watembenezira nsana wake kwa osonkhana—Mkonzi.]

¹⁹⁰ Kumbuyo kwanga, kuli munthu wakhala kumbuyo kwanga. Iye akukhudza Mulungu. Ndipo chimene iye akufuna; iye ali ndi mwana amene ali ndi vuto la mtima. Ndipo mwana uyo ali nako

kung'ung'uza mu mtima mwake, adotolo anatero. Ndipo dzina la munthu uyo ndi Bambo Cox. Imani, Bambo Cox. “Ndipo Iye anamuuza Sarah zomwe iye anali kuganiza, kuseri kwa Iye.”

[M'bale Branham apitiriza kulozetsa nsana wake kwa osonkhana—Mkonzi.]

¹⁹¹ Kulumphu kumene kanjira kuchokera kwa iye, kubwerera patsogolo pang'ono, pali mwamuna amene sakuchokera kuno, koma akuchokera ku New Mexico. Ine sindinamuwonepo iye, mmoyo wanga. Ine ndikuyang'ana kumene pa iye tsopano, ndipo iye ali kumbuyo kwanga. Iye akuchokera ku New Mexico. Ndipo mwamunayo ali ndi msungwana amene iye akukondweretsedwa naye, ndipo msungwanayo ali nacho chinachake cholakwika ndi kamwa yake. Ndicho... Khungu la mkamwa mwake ndi chimene chavuta. Ndipo dzina la mwamunayo ndi Bambo West. Kodi mungayime inu, bwana. Ndine mlendo kwathunthu kwa inu, koma Ambuye Mulungu amuchiza mwana wanu.

¹⁹² Kodi inu mukukhulupirira tsopano ndi mtima wanu wonse? [Osonkhana anena, “Ameni.”—Mkonzi.] Ndi angati a inu mukukhulupirira tsopano ndi mtima wanu wonse? [“Ameni.”] Tsopano, kodi sali Yesu Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse? [“Ameni.”] Kodi inu mukumulandira Iye tsopano ngati Mpulumutsi wanu? Kwezani dzanja lanu. [“Ameni.”] Kodi inu mukukhulupirira mwa Iye ngati Mchiritsi wanu? [“Ameni.”]

¹⁹³ Apa, apa pali munthu wakhala apa, wolumala kapena chinachake, wagona pa machira.

Kodi inu mukukhoza kundimva ine kupyolera cholankhulira ichi? [M'bale Branham akutenga cholankhulira nayenda molunjika ku mathero a nsanja nalankhula kwa mkazi ali pa machira—Mkonzi.] Ine sindikukudziwani inu. Ndinu chabe mkazi mutagona apo. Ngati ine ndingakhoze kukuchizani inu, ine ndikanadzachita icho. Ine sindingakhoze kukuchizani inu.

[Mwamuna ayamba kulira—Mkonzi.] Chabwino. Ndi munthu chabe amene akusangalala. Mwana wake anachiritsidwa.

Ine sindikukudziwani inu. Ndinu mkazi, ndipo ndine mwamuna. Iyi ndi nthawi yoyamba imene ife tinakomana mmoyo, ine ndikuganiza. Anthu awa...?... amene akubweretsani inu. Moona, iyi ndi nthawi yanu yoyamba kuno; anangokubweretsani inu mkati. Inu mwachokera njira yayitali. Inu muli ndi mthunzi wa ku imfa. Inu muli ndi khansala. Si kulumala. Ndi khansala. Adotolo sangakhoze kukuchitirani inu chinanso. Izo nzoona. Ndipo inu zedi mukufa; adotolo awo sangakhoze kukuchitirani inu chirichonse.

¹⁹⁴ Nthawi yina panali akhate atatu anakhala pa chipata cha Samaria. Ndipo akhate awo ananena, “Kodi ife tikhala pano mpaka ife tidzafe?” Chifukwa, matenda onse, kufa ndi njala, ndi kumadyerana ana. Iwo anati, “Ngati ife tipita ku msasa

wa adani, Asiriya; ngati iwo akatipha ife, ife tikafa, chonchobe. Ndipo ngati iwo akatipulumutsa ife, ife tidzakhala moyo.” Ndipo iwo anatenga mwayi uwo. Ndipo, mwa chikhulupiriro icho, iwo sanangodzipulumutsa okha koma gulu lonse.


¹⁹⁵ Tsopano, inu mufa ngati inu mukhala pamenepo. Koma inu simukufunsidwa kupita ku msasa umene iwo anapita. Koma inu mukuyitanidwa ku nyumba ya Atate. . . ? . . .

¹⁹⁶ Inu mukufa ndi khansala. Inu simungakhoze kukhala moyo kunja kwa Mulungu. Inu sindinu wochokera mu mzinda uno. Ndinu ochokera kozungulira kuno. Inu mwabwera njira yayitali. Ndinu ochokera ku Milwaukee. Izo nzoona. Uko nkulondola. Ine ndinawona mzinda. Ine ndikudziwa izo. Uko nkulondola.

Kodi inu mukukhulupirira izo? Kodi inu mulandira Mulungu tsopano ngati mchiritsi wanu? Ngati inu mutero, ziribe kanthu kaya inu muli ofooka chotani, kaya inu mwagona chotani pa bedi, ine ndikukhulupirira, mu vuto lanu, ine ndikanauka mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo tenga machira awo ndipo zipita kwanu, ndipo ukakhale moyo kwa ulemerero wa Mulungu. Kodi inu mundimvera ine, ngati mneneri wa Mulungu? Ndiye dzukani ndipo muzipita, ndipo khalani bwino. Khalani bwino! Musati muwope. Dzukani pa machira; Mulungu akupangani inu kukhala bwino. Mwaona?

¹⁹⁷ Wina amugwire iye kotero kuti iye akhoze kudzuka ndi kupeza mphamvu. Kodi inu mukukhulupirira Mulungu? Mungomulola iye apeze mphamvu pang’ono; iye akhala bwino. Ndi zimenezo, mlongo. Ndi uyo ali apo, mu Dzina la Ambuye Yesu! [Osonkhana asangalala pamene mlongo tsopano akuyima.]

Tiyeni ife tiyime ndi kupereka mayamiko kwa Mulungu. Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse! [Osonkhana akusangalala kwakukulu ndi kuyamikira Mulungu—Mkonzi.]

Pitani, ndipo Ambuye Yesu Khristu akudalitseni inu. [Osonkhana akupitiriza kusangalala kwakukulu ndi kuyamikira Mulungu—Mkonzi.] 

65-0221E Kodi Melkizedeki Uyu Ndi Ndani?
Parkview Junior High School
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©1995 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org